

Kuphunzira Buku La **YOHANE**



**Yesu anati kwa iye, Ine ndine kuuka ndi moyo:
wokhulupirira Ine, angakhale amwalira, adzakhala ndi
moyo.**

—Yohane 11:25

WABWINO WA YOHANE UNALEMBEDWA CHIFUKWA CHIYANI

Ndipo zizindikiro zina zambiri Yesu anazichita pamaso pa ophunzira ake, zimene sizinaleembedwa m'buku ili; koma zaleembedwa izi kuti mukakhulupirire kuti Yesu ndiye Khristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupirira mukhale nao moyo m'dzina lake.

—Yohane 20:30, 31

Yohane ankadzitchula yekha kuti anali “Wophunzira amene Yesu anamkonda.” Sitikuganiza kuti Yesu anamukonda Yohane koposa ophunzira ena onse. Koma mwina Yohane ndi amene ankamvetsa kwambiri za chikondi cha Yesu chimeñe chinali pa ophunzira onse. Yohane ankayamika chikondi cha Yesu kwambiri komanso cholinga cha Yesu kudziko lapansi.

Patapita zaka zambiri chilembedwere uthenga Wabwino wa Mateyu, Marko ndi Luka, ziphunzitso zonyenga zinayamba kufalikira nkumati Yesu anali munthu wamba. Chifukwa cha ichi, Yohane analemba buku lapadera pofuna kuonetsa kuti Yesu anali Mulungu wokhala ndi thupi la umunthu. Mwa zodabwitsa mazana mazana zimene Yesu anazichita, Yohane anasankha mosamalitsa zokhazo zomwe zinkatsimikiza kuti Yesu analidi uyo YEMWE ankadzifotokozeria yekha. Zozizwitsa zimenezo anazitcha kuti “Zizindikiro”.

Yohane anatsimikizirango zifukwa zimene akuluakulu a zipembeedzo ankamudera Yesu namupereka kuti apachikidwe. Chinali chifukwa chakuti Yesu ankanena kuti anali wofanana ndi Mulungu! Yohane akuonetsa zomwe Yesu anakonza kuti akhale “Mwanawankhosa wa Mulungu”

wakuchotsa machimo a dziko lapansi. Yesu anadzipereka yekha ngati nsembe yenyeni yovomerezeka ndi Mulungu pofuna kuwombola dziko lapansi ku machimo.

Chinali cholina cha Yohane kuti onse owerenga uthenga wake ("uthenga wabwino") akhulupirire Yesu ndi kulantira moyo wosatha.

Ndi pemphero langa kuti phunziro ili la Uthenga Wabwino monga analembera Yohane likuthandizirani kukhulupirira mwa Yesu ndi kumulantira mumtima mwanu kuti akhale mpulumutsi ndi Ambuye wanu. Yesu ndi moyo ndipo akufuna kugawana nanu moyo umenewu kwamuyaya. Bwanji mumuuze lero kuti mukusya moyo wanu wakale ndi kumulantira lye! Mumuyamike chifukwa cha moyo watsopano womwe wakupatsani. Mukondwere nacho chiyanjano chanu ndi lye pamoyo wanu wa tsiku ndi tsiku ndipo muwauzenso ena za Yesu wodabwitsayo. Nawonso awakonda.

—V. R. Benson

MUNGAPHUNZIRE BWANJI MAU A MULUNGU



- 1. Pempherani kuti Mulungu akuthandizeni.** Mufunika kuthandizi-dwa ndi Mulungu kuti mumvetsetse zomwe mukuphunzira mu Baibulo. Mau opezeaka pa Masalimo 119:18 muwaone ngati pemphero: “**Munditsegulire maso, kuti ndipenye zodabwitsa za m'chilamulo chanu.**”
- 2. Muwerenge malemba mosa-malitsa komanso pa malo popanda phokoso.** Mudzilemba mzere pansi pa mau omwe akukugwirani mtima. Kumbukirani kuti Mulungu amalankhu-la nanu kudzera mu mau ake.
- 3. Mudziyankha mafunso opeze-ka mu mau omwe mwawerenga.**
- 4. Muone mayankho opezeaka mkati mwa chikuto cha kumapeto.**
- 5. Lowezani pamtima mavesi omwe mwapatsidwa.** Muwerenge kangapo mofuula mau oloweza pamtima kufikira atakhazikika mpaka muthe kuwanena osaonera. Mukhoza kulembanso mau olwezao ndi vesi yake pa kapepala kuti mudzitha

kuyenda nako kulikonse. Mudzinena mofuula mauwo kanganapo kuti muthe kuwakumbukira. Muwanene mauwo kwa mnzanu yemwe angathe kukuuzani pomwe mukulakwitsa. Mukhozanso kulemba mauwo osaonera pambuyo pake nkufanizira ndi momwe alembera mu buku pofuna kutsimikiza kuti mau omwewo mwawalemba bwino. Muwawerenge mauwo kamodzi pa sabata kwa masabata asanu ndi awiri (7) kenako, kamodzi pa mwezi. Pamene mukusunga "chuma ichi" mumtima mwanu, mau ndi zochita zanu zidzakhala zosinthika. Sankhani mau ena a mu Baibulo kuti muwalowezenso.

6. Muganizire mau a Mulungu amene mwawerenga, kuphunzira ndi kuloweza pamtima. Mulungu amapanga malonjezano apadera ndi iwo amene amatenga nthawi yolingalira mau ake usana ndi usiku:

Buku ili la chilamulo lisachoke pakamwa pako; koma ulingiriremo usana ndi usiku, kuti usamalire kuchita monga mwa zonse zolembedwamo; popeza ukatero udzakometsa njira yako, nudzachita mwanzeru.

—Yoswa 1:8

Komatu m'chilamulo cha Yehova muli chikondwerero chake; ndipo m'chilamulo chake amalingirira usana ndi usiku. Ndiye akunga mtengo wooka pa mitsinje ya madzi; wakupatsa chipatso chake pa nyengo yake, tsamba lake lomwe losafota; ndipo zonse azichita apindula nazo.

—Masalimo 1:2, 3

7. Chitani zimene Mulungu akunena. Yakobo 1:22 akutiua kuti, “**Khalani akuchita mau, osati akumva okha, ndi kudzinyenga nokha.**” Yesu anafanizira munthu amene amamva mau ake koma osawachita kuti ali ngati munthu wopusa amene anamanga nyumba yake pa mchenga. Pamene mphepo ndi mvula ndi kusefukira kwa madzi kunafika, nyumbayo inagwa. Koma bambo kapena mai, mnyamata kapena mtsikana amene amamva mau a Yesu *nawachita* ali ngati munthu wanzeru, amene anamanga nyumba yake pa thanthwe. Pamene mphepo ndi mvula ndi kusefukira kwa madzi zinafika, nyumbayo inaima njii chifukwa inamangidwa pa thanthwe. Ndi pokhapo pamene *tichita* zimene Mulungu anena pamene tingakule muuzimu ndi kumudziwa bwino Mulungu. Lembani zenizeni zimene mukufuna kuchita, ndipo kenaka muzichite. Mulungu akhala nanu, ndi akuthandizani.


8. Gawanani mau a Mulungu ndi munthu wina. Mukhoza kugawana zimene mwaphunzira ndi anzalu a pabanja panu. Deuteronomo 6:7 akunena kuti, “**Ndipo muziwaphunzitsa mwachangu kwa ana anu, ndi kuwalankhula awa pokhala pansi m’nyumba zanu, ndi poyenda inu panjira, ndi pogona inu pansi, ndi pouka inu.**”

PHUNZIRO 1. MAU OPAMBANA OFOTOKOZA ZA YESU KHRISTU

Yohane 1:1-18

¹Pachiyambi panali Mau, ndipo Mau anali kwa Mu-

lungu, ndipo Mau ndiye Mulungu. ²Awa anali pachiyambi kwa Mulungu. ³Zonse



zinalengedwa ndi Iye; ndipo kopanda Iye sikunalengedwa kanthu kalikonse kolengedwa. ⁴Mwa Iye munali moyo; ndi moyowu unali kuunika kwa anthu. ⁵Ndipo kuunikaku kunawala mumdimia; ndi mdimawu sunakuzindikira.

⁶Kunali munthu, wotumidwa ndi Mulungu, dzina lake ndiye Yohane. ⁷Iyeyu anadza mwa umboni kudzachita umboni za kuunikaku, kuti onse akakhulupirire mwa iye. ⁸Iye sindiye kuunikaku, koma anatumidwa kukachita umboni wa kuunikaku. ⁹Uku ndiko kuunika kwenikweni, kumene kuunikira anthu onse akulowa m'dziko lapansi.

¹⁰Anali m'dziko lapansi, ndi dziko linalengedwa ndi Iye, koma dziko silinamzindikira Iye. ¹¹Anadza kwa zake za Iye yekha, ndipo ake a mwini yekha sanamlandire Iye. ¹²Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, aku-khulupirira dzina lake; ¹³amene sanabadwe ndi mwa-ziz, kapena ndi chifuniro cha thupi, kapena ndi chifuniro cha munthu, koma cha Mulungu. ¹⁴Ndipo Mau anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife, ndipo tinaona ulemerero wake, ulemerero wonga wa wobadwa yekha wa Atate, wodzala ndi chisomo ndi choonadi.

¹⁵Yohane achita umboni za Iye, nafuula nati, Uyu ndiye amene ndinanena za Iye, Wakudzayo pambuyo panga analipo ndisanabadwe ine; chifukwa anakhala woyamba wa ine. ¹⁶Chifukwa mwa kudzala kwake tinalandira ife tonse, chisomo chosinthana ndi chisomo. ¹⁷Chifukwa chi-

lamulo chinapatsidwa mwa Mose; chisomo ndi choonadi zinadza mwa Yesu Khristu.
18Kulibe munthu anaona

Mulungu nthawi zonse; Mwana wobadwa yekha wakukhala pa chifuwa cha Atate, Iyeyu anafotoko zera.

Zoti muchite

A. Mulembe yankho lanu pa funso lili lonse lomwe lili m'munsimo. Ngati mutalephera kuyankha funso muwere-ngenzo phunziro la Baibulo.

1. Ndani yemwe anali "Mau"? _____ (vesi 1)

2. "Mau" anali kuti? _____ (1)

3. "Mu Mau" Munali chiyani? _____ (4)

4. Kuunika kunaunikira kuti? Mu _____ (5)

5. Ndani anatumidwa ndi Mulungu kudzachitira umboni za kuunika? Munthu wotchedwa _____ (6)

[Ameneyu anali Yohane M'batizi, osati Yohane yemwe analemba uthenga wabwino.]

6. Ndani amene sanamulandire Yesu? _____ (11)

[Israele, monga mtundu wa anthu osankhika ndi Mulungu, sanavomereze Khristu.]

7. Ndimphamu yotani yomwe anthu omulandira Yesu amapatsidwa? Mphamu yakukhala _____ (12)

8. Iwo akubadwa mwa Mulungu sakhala _____ kapena a chifuniro cha _____

_____ kapena a chifuniro cha _____ koma cha _____ (13)

[Munthu akakhala mwana wa Mulungu, chimakhala chozizwa chomwe Mulungu amapanga. Chozizwachi sichichitika chifukwa chobadwira mu banja la chikhristu, kapena chifukwa chakuti inuyo mwangofuna kuti zitero. Sizichitikanso chifukwa chakuti wina wafuna kuti inuyo mubadwenso mwatsopano. Ntchito yakubadwa mwatsopano amaigwira ndi Mulungu.]

9. "Mau" anakhala chiyani? _____ (14)
10. "Mau" anakhala kuti? _____ (14)
11. Ndi zinthu ziwiri ziti zomwe timalandira pamene tiri ndi Khristu? Chifukwa mwa _____ tinalandira ife _____, [chisomo chake chotsatana] (16).
12. Chifukwa chakuti palibe munthu amene anamuona Mulungu, ndani amene anabwera kudzatiuza kuti Mulungu ndi ndani? _____ (18).

[Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu, amakhala padziko lapansi komanso nthawi yomweyo anakhalapo chiyambire cha dziko.) (Tasiyanitsani mau opezeka pa Vesi 18 ndi Vesi 1.)]

B. Mulembe ndi kuloweza pamtima mau opezeka pa:
Yohane 1:12

Yesu ndi Mulungu—anadza ndi thupi la umunthu

Tisanamulandire Yesu ndi kukhulupirira dzina lake, tiyenera kumudziwa kuti *lye ndi ndani*. Vesi 18 ikunena kuti Yesu anabwera kudzationetsa Mulungu chifukwa panalibe amene anamuyandikirapo Mulungu ndi kumuona kwathunthu. Ulemerero wa Mulungu ndi owala kwambiri. *lye ndi oyera kwambiri.*

Chifukwa chakuti munthu ndi wochimwa, iye amakhala mu mdima wauzimu. Dziko lapansi lomwe sililabadira Mulungu ndipo limayesera kukhala lopanda Mulungu ndilo

mdima umenewo. Koma tikuona pa vesi 5 kuti mdima unalephera kugonjetsa kuunika.

Baibulo limanena kuti, “**Ndipo uwu ndi uthenga tidaumva kwa lye, ndipo tiulalikira kwa inu, kuti Mulungu ndiye kuunika, ndipo mwa lye monse mulibe mdima**” (1 Yohane 1:5). Yesu yemwe ali Mulungu, ankatchedwa “**kuunika kwenikweni**” (Yohane 1:9). Munthu amakhoza kudziona monga m’mene *alili* ngati wochimwa. Ndipo “**kuunika kwenikweni**” akhozanso kumuona Mulungu monga momwe *alili*. Akhozanso kuona momwe munthu ayenera kukhalira.

Ndi chinthu chopambana kuti Yesu, yemwe ndi kuunika kwenikweni amaunikira dziko lapansi lomwe ndi lamdimma, kuti atiwonetse Mulungu! Monga m’mene ananenera mtsikana wina wamng’ono kuti, “Yesu ndiye chithunzi chopambana chimene Mulungu anajambula!” Yesu ndiye chithunzi cha Mulungu—Amene anthu anakatha kumuona, kumumva akuyankhula komanso kumukhudza.

Yesu *anakhala* pakati pa anthu. Mau oti “*anakhala*” pa vesi 14 akutanthauza kuti “*anakhala ngati hema*.” Yesu *anakhala ngati chihema* pakati pa anthu. Chihema chomwe timachimva mu Chipangano Chakale, chinali ngati tchalichi cha msasa (tent) chomwe Mulungu anachimanga chomwe a Israele anakatha kumayenda nacho akamasamukira ku malo osiyana siyana. Kachisi yemwe patsogolo pake anadzakhala nyumba yaikulu yokhazikika yopembedzeramo ku Yerusalem, anali malo omwe AMBUYE Mulungu anakhalamo ndi anthu ake osankhika. Pambuyo pake a Israele atachimwa, ulemerero wa Mulungu unachokamo mu kachisimo. Koma tsopano, kudzera mwa Yesu Khristu, Mulungu wabwereranso mu “Kachisi” ndi kukhalanso ndi anthu ake. Kodi simukuona kuti anthu ambiri sanamuzindikire lye? Koma iwo amene anakhulupiriradi mwa Mulungu anaona ulemerero wa Mulungu atabwera Yesu (vesi 14).

Yesu ndiye mau a Mulungu

Baibulo limanena kuti, “**Mau anu ndiwo nyali ya ku mapazi anga, ndi kuunika kwa panjira panga**” (Masalimo 119:105). Dzina lina la Yesu ndilo “Mau a Mulungu.” (Tafananizani mau opezeka pa vesi 1 ndi pa vesi 14.) Buku Lopatulika ndi mau a Mulungu olembedwa. Yesu ndi “*Mau a moyo*” a Mulungu, chifukwa Mulungu amadzifotokozerwa lye mwini kudzera mwa Yesu.

“Kale Mulungu analankhula ndi makolo mwa aneneri m'manenedwe ambiri ndi mosiyanasiyana, koma pakutha pake pa masiku ano analankhula ndi ife ndi Mwana amene anamuika wolowa nyumba wa zonse” (Ahebri 1:1, 2a).

Yesu ndiye moyo wa Mulungu

Kodi munayamba mwaganizira kuti ndi chifukwa chiyani timakhala ana a Mulungu tikalandira Yesu Khristu m'mitima mwathu? Chifuwa chake ndi chakuti, “**Mwa lye munali moyo**” (vesi 4).

Choyamba tikuona kuti Yesu analenga zamoyo zonse (mavesi ndi 10). “**Zinthu zonse zinalengedwa mwa lye ndi kwa lye. Ndipo lye ali woyamba wa zonse, ndipo zonse zigwirizana pamodzi mwa lye**” (Akolose 1:16b, 17). Yesu, monga Mulungu, ndiye gwero la moyo ndipo amachilikiza zamoyo zonse. “**Popeza lye mwini apatsa zonse moyo ndi mpweya ndi zinthu zonse**” (Machitidwe A Atumwi 17:25b). “**Pakuti mwa lye tikhala ndi moyo ndi kuyendayenda, ndi kupeza mkhalidwe wathu**” (Machitidwe A Atumwi 17:28a).

Monga momwe munthu anakhalira Mzimu wamoyo pomwe Mulungu anapumira mpweya wamoyo mu mphuno mwake polenga dziko lapansi, chimodzimodzinso Yesu wapatsidwa mphamvu pathupi lililonse, moyo (wauzimu)

wosatha kwa onse obwera kwa iye (Yohane 17:2). “**Iye wakukhala ndi Mwana ali nao moyo; wosakhala ndi Mwana wa Mulungu alibe moyo**” (1 Yohane 5:12).

Kodi munalandira—moyo wauzimu—pomulandira Yesu ndi kukhulupirira kotheratu dzina lake? Ngati munachita izi, ndinu mwana wa Mulungu, wobadwanso mwa Mulungu, ndipo munalandira moyo wosatha. Pamene mukuyenda mkuwala kwake ndikumva moyo wake mwa inu, mudzalandira madalitso ambiri (vesi 16). Ngati musanamulandire, bwanji osamupempha kuti alowe mumtima mwanu ndi kukupatsani moyo watsopano—moyo wake wosatha?

Kodi mudayamba mwavomera inu wina atagogoda pakhommo la nyumba yanu? Yesu waima pafupi nanu tsopano, ndipo akugogoda pakhommo lamtima wanu. Akulonjeza kuti, “**Wina akamva mau anga nakatsegula pakhommo, ndidza-lowa kwa iye, ndipo ndidzadya naye, ndi iye ndi Ine**” (Chivumbulutso 3:20).

PHUNZIRO 2. YOHANE M'BATIZI AKONZA NJIRA A YESU

Yohane 1:19-34

¹⁹Ndipo umene ndiwo umbo-ni wa Yohane, pamene Ayuda anatuma kwa iye ansembe ndi Alevi a ku Yerusalemu aka-mfunse iye, Ndiwe yani?


²⁰Ndipo anavomera, wosaka-na; nalola kuti, Sindine Khristu. ²¹Ndipo anamfunsa iye, Nanga bwanji? Ndiwe Eliya

kodi? Nanena iye, Sindine iye. Ndiwe Mneneriyo kodi? Na-yankha, Iai. ²²Chifukwa chake anati kwa iye, Ndiwe yani? Kuti tibwezere mau kwa iwo anatituma ife. Unena chiyani za iwe wekha? ²³Anati, Ndine mau a wofuula m'chipululu, Lungamitsani njira ya Mbuye, monga anati Yesaya mne-



neriyo. ²⁴Ndipo otumidwawo anali a kwa Afarisi. ²⁵Ndipo anamfunsa iye, nati kwa iye, Koma ubatiza bwanji, ngati suli Khristu, kapena Eliya, kapena Mneneriyo? ²⁶Yohane anawayankha, nati, Ine ndi-
batiza ndi madzi; pakati pa inu paimirira amene simu-
mdziwa, ²⁷ndiye wakudza pambuyo panga, amene sindi-
yenera kummasulira lamba la nsapato yake. ²⁸Zinthu izi zi-
nachitika m'Betaniya tsidya lija la Yordani, pomwe anali-
kubatiza Yohane. ²⁹M'mawa mwake anaona Yesu alinku-
dza kwa iye, nanena, Onani Mwanawankhosa wa Mulun-
gu amene achotsa tchimo

lake la dziko lapansi! ³⁰Ndiye amene ndinati za Iye, Pambu-
yo panga palinkudza munthu amene analipo ndisanabadwe ine; pakuti anali woyamba wa ine. ³¹Ndipo sindinamdziwa Iye; koma kuti aonetsedwe kwa Israele, chifukwa cha ichi ndinadza ine kudzabatiza ndi madzi. ³²Ndipo Yohane ana-
chita umboni, nati, Ndinaona Mzimu alikutsika kuchokera Kumwamba monga nkunda; nakhalabe pa Iye. ³³Ndipo si-
ndinamdziwa Iye, koma wo-
nditumayo kudzabatiza ndi madzi, Iyeyu ananena ndi ine,
Amene udzaona Mzimu atsi-
kira, nakhala pa Iye, yemwe-
yu ndiye wakubatiza ndi Mzi-
mu Woyer. ³⁴Ndipo ndaona ine, ndipo ndachita umboni
kuti Mwana wa Mulungu ndi Yemweyu.



Zoti muchite

Mulembe mau oyenera m'malo mosalembedwamo.

1. Yohane Mbatizi ananena kuti iye anali _____
a munthu wofuula _____ (23).
2. Yohane M'batizi ananena mau omwe ananenera Yesaya onena kuti, "Lungamitsani _____ Ambuye" (23).
3. Yohane ananena kuti ngakhale Yesu amabwera _____ pake, iye anali _____ (27, 30).

[Izi zikutanthauza kuti ngakhale Yohane M'batizi anabwera kudzakonza njira ya Yesu, Yesu ndiye anali wopambana kwambiri. Yohane ananena kuti iye sanayenera kugwira ngakhale ntchito ya kapolo yomasula zingwe za nsapato za Yesu. Yohane anazindikira kupambana kwa Yesu.]

4. Yohane atawalozera anthu onse kwa Yesu, anamutchula kuti _____ wa _____ chifukwa Yesu ndi yemwe akanachotsa _____ la _____ (29).

5. Yohane anadza kudzabatiza anthu ndi madzi kuti Yesu akaonet sedwe kwa _____ (31).

6. Yohane anadziwa kuti Yesu anali mwana wa Mulungu (Mulungu wobadwa ngati munthu) chifukwa Mzimu wa Mulungu unadza pa dziko lapansi kuchokera kumwamba monga _____ ndikutera pamutu pa Yesu (32). Ichi chinali chizindikiro chakuti Yesu adzabatiza ndi _____ (33).

Kukonza njira ya Yesu

Mtundu wosankhika a wa Mulungu, Israele unakhala wopanda m'neneri kwa zaka 400 wochokera kwa Mulungu. Anali *nacho* Chipangano Chatsopano chowauza zomwe Mulungu ankafuna komanso malonjezano ake. Ankadziwa kuti Mesiya, mombolo wodzozedwa ndi Mulungu, adzabwera

tsiku lina kudzalamulira Israele. Yesaya ananena kuti m'neneri ameneyu adzabadwa mwa namwali, (Yesaya 7:14) namutcha dzina lake Imanuele kutanthauza kuti "Mulungu nafe." Mika ananeneratu kuti m'neneri ameneyu adzabdwira ku Yerusalemu ndipo adzakhala wolamulira Israele (Mika 5:2).

Kodi simukuona kuti anthu anali odabwa komanso kuskondwera pomva Yohane M'batizi akuwauza kuti akonzekere kubwera kwa Ambuye? Anthu *anayenera* kukonzekera bwanji? Mateyu akutiuba kuti Yohane analalikira nati, "**Tembenukani mitima; chifukwa Ufumu wa Kumwamba wayandikira**" (Mateyu 3:2). Yohane anabatiza anthu ambiri mu mtsinje wa Yordano, "navomereza machimo ao." Mukhoza kuona kuti mitima isanakonzeke kulandira Yesu, iyenera kuvomereza ndi kusiya machimo (kulapa). Pamene inu ndi ine tavomereza kusiya machimo athu—maganizo athu oipa, komanso ntchito zathu zoipa pamaso pa Mulungu ndi munthu mnzathu—pamenepo *ndi* pamene tingavomereza Yesu ngati "njira" yopitira kwa Mulungu ndipo tikhoza kumulandira lye ngati mfumu ndi Ambuye. Ubatizo wa Yohane M'batizi womwe unali wa m'madzi unali wolozera kukhululukidwa ku machimo. Yesu ankabwera kudzabatiza ndi Mzimu Woyeru pochotsa machimo ndi moto (Mateyu 3:11, 12). Ndikutipatsa moyo watsopano wa chiyeretso (moyo wa Khristu mwa ife). Kodi mwavomereza machimo *anu* kwa Mulungu?

Yesu mwanawankhosa wa Mulungu

Anthu a ku Israele ankadziwa kufunikira kwa nkosa pa kukhala kwao ndi Mulungu. Panali patapita zaka zambiri kuchokera pomwe ana a Israele anali mu ukapolo ku Ejipito. Mulungu anasintha mtima wa Farao kuti alole kuti anthu a Mulungu atuluke ku Ejipito ngati afulu. Mulungu anagwiritsa

ntchito miliri khumi kuti Farao avomere anthu ambiriwo omwe analipo pafupifupi 2 miliyoni kuti atuluke. Mliri womaliza komanso owawitsa unali wakuti Ambuye adutse mu dziko lonse la Ejipito ndi kupha usiku umodzi ana onse oyamba kubadwa.



Panali njira yopulumukira.

Mulungu analamula kuti kuphedwe mwanawankhosa wopanda banga. Mwazi wa mwanawankhosayo anati awazidwe pa khomo la nyumba. Anati Mulungu akaona mwaziwo, "adzadutsa" ndipo Mulungu sadzawaononga. Ichi ndiye chinalidi chikonzero chopambana! Ana a Israele anayenera kuchita madyerero a Paska (kudutsa) chaka chili-chonse ngati chikumbutso cha nthawi imene chiweruzo cha Mulungu "chinadutsa" chifukwa chopaka mwazi wa nkosa pa makomo ao. (Nkhaniyi ikupeze ka pa Eksodo 12:1-42.)

Koma ndiyetu ndi chinthu chamtengo wapatali kufotokoze-ra za Yesu ku gulu la anthu ndi mau oti, "Mwanawankhosa wa Mulungu"! Anadza kudzakhala mwanawankhosa wodza-perekedwa nsembe, wamphumphu, wopanda banga kape-nanso tchimo, kuti mwazi wake wokhet sedwa upakidwe pa mitima yathu kuti chiweruzo cha Mulungu chakudza chifu-kwa cha machimo athu "chidutse" ndikutipitilira ife! Ahebri 9:22 akuti uza kuti "...ndipo wopanda kukhetsa mwazi palibe [kukhululukidwa kwa machimo]." Levitiko 17:11 amena kuti, "...Pakuti wochita chotetezera ndiwo mwazi, chifukwa cha moyo wake." Anaankhosa onse omwe anaperekedwa nsembe mzaka zonse anali kulozera kwa Yesu amene anayenera kubwera ngati "mwanawankhosa

wa Mulungu" kudzakhetsa mwazi wake kuti onse omulandira ngati mpulumutsi mwazi wake upakidwe pa makomo a mitima yao. "Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti iye wakumva mau anga, ndi kukhulupirira lye amene anandituma lne, ali nao moyo wosatha, ndipo salowa m'kuweruza, koma wachokera kuimfa, nalowa m'moyo" (Yohane 5:24).

Yesaya 53:7 akunena kuti, "**Ngati nkhosa yotsogolere-dwa kukaphedwa.**" Yesu anadza kudzafera machimo a dziko lapansi. Bwanji osamuyamika mokweza mau nthawi yomwe ino chifukwa chokhala mwanawankhosa wa Mulungu, yemwe mwazi wake unakhet sedwa chifukwa cha *inu* kuti uku-chotsereni machimo *anu*. Mulungu akaona mwazi, saonanso machimo *anu*. Amangoona nsembe yovomerezeka ya chikhristu yomwe anatichotsera machimo nalandira chiweru zo m'malo mwathu. Alemekezedwe Mulungu!

UFUNA KUWOMBOLEDWA KODI?

Ilipo mphamvu m'mwazi wake;
Ufuna kugonjetsa zoipa?
Muli mphamvu m'mwazi wake



**Kuchita chopepesera machimo kumatanthauza
kukhala pamodzi ndi Mulungu, popeza mwazi
wa Yesu unatiyeretsa ife ku machimo athu.**

PHUNZIRO 3. KUMUDZIWA YESU



Yohane 1:35-49

³⁵M'mawa mwakenso anali-
kuimirira Yohane ndi awiri a
ophunzira ake; ³⁶ndipo poya-
ng'ana Yesu alikuyenda, anati,
Onani Mwanawankhosa wa
Mulungu! ³⁷Ndipo ophunzira

awiriwo anamva iye alinkulankhula, natsata Yesu.³⁸Koma Yesu anacheuka, napenya iwo alikumtsata, nanena nao, Mufuna chiyani? Ndipo anati kwa Iye, Rabi (ndiko kunena posandulika, Mphunzitsi), mukhala kuti?³⁹Nanena nao, Tiyen, mukaone. Pamene po anadza naona kumene anakhala; nakhala ndi Iye tsiku lomwelo; panali monga ora lakhumi.⁴⁰Andrea mbale wake wa Simoni Petro anali mmodzi wa awiriwo, anamva Yohane, namtsata Iye.⁴¹Anayamba iye kupeza mbale wake yekha Simoni, nanena naye, Tapeza ife Mesiya (ndiko kusandulika Khristu).⁴²Anadza naye kwa Yesu. M'mene anamyang'ana iye, anati, Uli Simoni mwana wa Yohane; udzatchedwa Kefa (ndiko kusandulika Petro).

⁴³M'mawa mwake anafuna kutuluka kunka ku Galileya, napeza Filipo. Ndipo Yesu ananena naye, Tsata Ine.⁴⁴Koma Filipo anali wa ku Betsaida, mudzi wa Andrea ndi Petro.⁴⁵Filipo anapeza

Natanaele, nanena naye, Iye amene Mose analembera za Iye m'chilamulo, ndi aneneri, tampeza, ndiye Yesu mwana wa Yosefe wa ku Nazarete.⁴⁶Natanaele anati kwa iye, Ku Nazarete nkutha kuchokera kanthu kabwino kodi? Filipo ananena naye, Tiye ukaone.⁴⁷Yesu anaona Natanaele alinkudza kwa Iye, nanena za iye, Onani, Mwisraele ndithu, mwa iye mulibe chinyengo!⁴⁸Natanaele ananena naye, Munandidziwira kuti? Yesu anayankha nati kwa iye, Asanakuitane Filipo, pokhala iwe pansi pa mkuyu paja, ndinakuona iwe.⁴⁹Natanaele anayankha Iye, Rabi, Inu ndinu Mwana wa Mulungu, ndinu mfumu ya Israele.



Bwerani mudzaone

Ophunzira awiri a Yohane M'batizi anali ndi chidwi chofuna kudziwa zambiri za Yesu pamene anamva Yohane akunena kuti, "Onani Mwanawankhosa wa Mulungu!" Anaganiza zofufuza komwe Yesu ankakhala. Yesu anawaitana nati, "Bwerani mudzaone." Tangoganizirani kupambana kwa zokambiranana zao ndi Yesu, chifukwa pambuyo pake m'modzi wa anthuwo yemwe dzina lake ndi Andreya, ana-muuza m'bale wake Petro kuti adamupeza Mesiya!

Dzina loti Mesiya limatanthauza kuti "Wodzozedwa" munthu yemwe anayenera kutumizidwa ndi Mulungu ngati m'neneri, wansembe, komanso mfumu yodzalamulira Israele. Aneneri ambiri a m'Chipangano Chakale adalankhulapo za munthu wopambanayu yemwe anamuyembekezera kuti abwera. Ngakhale Mose yemwe analemba za iye. Mulungu anamuua Mose kuti, "**Ndidzawaukitsira mneneri wa pakati pa abale ao, wonga iwe; ndipo ndidzampatsa mau anga m'kamwa mwake, ndipo adzanena nao zonse ndimuuzazi**" (Deuteronomo 18:18). Pambuyo pake Yesu anati, "**Koma monga anandiphunzitsa Atate, ndilankhula izi**" (Yohane 8:28b). Chinali chisangalalo chachikulu kwa amuna amenewa!

Kodi mukuchita naye chidwi Yesu? Mukufuna kuphunzira zambiri za Iye? Kodi nthawi zina mumadzifunsa kuti Yesu ndi ndani? Lero Yesu akukuuzani kuti, "Bwerani mudzaone." Pamene tifunafuna ndi pamene timapeza chachilendo. Yesu anati, "**Funani, ndipo mudzaopeza**" (Mateyu 7:7b). Ngati *mutabwera* kwa Yesu, *mudzaona!* Ngati mutakhala naye ndikumulola, ndi kumulola kuti alankhule nanu kudzera mwa mau ake, adzadzionetsera yekha kwa inu. Mudzamudziwa nokha. "**Ndipo ndidzapatsa iwo mtima wakundidziwa,**

kuti ndine Yehova, nadzakhala anthu anga, ndipo Ine ndidzakhala Mulungu wao; pakuti adzabwera kwa Ine ndi mtima wao” (Yeremiya 24:7).

Maumboni onena za Yesu

Munthu akabwera kwa Yesu namudziwa, amafuna atau-zanso ena za lye. Amafunitsitsa atauza ena zomwe akuzi-dziwa za Yesu, kuti enanso “abwere ndi kudzamuona.” Ngati mukumudziwa Yesu, ndipo mukuphunzira kuchokera kwa lye, kodi mukugawana Uthenga Wabwinowu ndi anthu ena?

Lembani mu mizere ili m'munsimu kuti Yesu ndi ndani kwa inu:

Mumpemphe Mulungu akupatseni mwai olankhula ndi ena za lye lero, kuti munthuyonso “abwere adzaone.”

PHUNZIRO 4. YESU AMABWERETSA CHIMWEMWE M'BANJA

Yohane 2:1-11

¹Ndipo tsiku lachitatu pa-nali ukwati m'Kana wa m'Ga-lileya; ndipo amake wa Yesu anali komweko. ²Ndipo Yesu yemwe ndi ophunzira ake anaitanidwa kuukwatiwo. ³Ndipo pakutha vinyo, amake

wa Yesu ananena naye, Alibe vinyo. ⁴Yesu nanena naye, Mkazi, ndili ndi chiyani ndi inu? Nthawi yanga siinafike. ⁵Amake ananena kwa atumi-ki, Chimene chilichonse aka-nena kwa inu, chitani. ⁶Ndipo panali pamenepo mitsuko



yamiyala isanu ndi umodzi yoikidwako monga mwa mayeretsedwe a Ayuda, yonse ya miyeso iwiri kapena itatu. ⁷Yesu ananena nao, Dzazani mitsukoyo ndi madzi. Naidzaza, ndendende. ⁸Ndipo ananena nao, Tungani tsopano, mupite nao kwa mkulu

wa phwando. Ndipo anapita nao. ⁹Koma pamene mkuluyo analawa madzi osanduka vinyowo, ndipo sanadziwe kumene anachokera (koma atumiki amene adatunga madzi anadziwa), mkuluyo anaitana mkwati, ¹⁰nanena naye, Munthu aliyense amayamba kuika vinyo wokoma; ndipo anthu atamwatu, pame nepo wina wosakoma; koma iwe wasunga vinyo wokoma kufikira tsopano lino. ¹¹Chi yambi ichi cha zizindikiro zake Yesu anachita m'Kana wa m'Galileya naonetsera ulemerero wake; ndipo ophunzira ake anakhulupirira Iye.

Zoti muchite

Mumizere yosaleembedwamo mulembe mau oyenera omwe mwaphunzira mu phunziroli.

1. Amai a Yesu anaauza anyamata amene atumikira kuti "

" (vesi 5).
2. Yesu atawauza anyamatayo kuti dzazani mbiyazi, iwo anadzaza " _____" (7).

Chimwemwe chimabwera ngati tiri omvera

Mai ake a Yesu anali asanamuone Yesu akuchita zodabwitsa chiyambire. Komabe amadziwa kuti Yesu akhoza ku-chita *chinachake* kuti awathandize. Tsopano tikudziwa kuti vinyo yemwe ankaperekedwa ku ukwatiwo si wamasiku anoyu yemwe anthu amaledzera naye. Analii chakumwa chotsekemera chopangidwa kuchokera ku mpesa. Zinali zokhumudwitsa mpaka vinyo kutha!

Mwina ndinu mukhristu. Kodi zina zinayamba “zakutherani” chiyambire? Kodi nthawi zina mtima wodekha umakuchokerani dzuwa lisanalowe? Kodi mtima wanu ndi wopanda chimwemwe kapena chikondi nthawi ino? Yesu akhoza kuona chosowa chanu chilichonse. Akufuna kudalitsa moyo wanu ndi chozizwa! Sakufuna muchititsidwe manyazi pa moyo wanu wa chikhristu posakhala ndi chimwemwe, mtendere ndi chikondi zokwanira tsiku lonse. Iye analonjeza kuti, **“Ndipo wakukhulupirira iye sadzachita manyazi”** (Aroma 9:33b). Koma pali *chinsinsi chimene mukuyenera kuchidziwa!* Kumvera kumatibweretsera madalitso. **“Chimene chilichonse akanena kwa inu, chitani”** (Yohane 2:5b). Tikakhala omvera Yesu akhoza kuchita zo-zizwa. Kumvera kumaonetsa kuti timakhulupiriradi iye.

Ngati wina anakulakwirani, kodi munamukhululukira munthu ameneyo? (Mateyu 6:14, 15) Kodi mukuunjika chuma chanu kumwamba (Mateyu 6:20)? Mwina mumaona ngati simungathe kuperekwa chuma ku ntchito ya Mulungu. Koma Yesu akudziwa zosowa zanu. Mumukhulupirire iye pomumvera **“Mundiyese nako tsono, ati Yehova wa makamu, ngati sindikutsegulirani mazenera a kumwamba, ndi**



kukutsanulirani mdalitso wakuti adzasoweka maloakuulandira” (Malaki 3:10b).

Mulungu akukuuzani lero kuti “**Komatu mudzale naye Mzimu**” (Aefeso 5:18b). Palibe mkhristu amene angaye-mbekezere kukhala moyo wa chisangalalo ngati salola Mulungu kumudzaza ndi Mzimu Woyerwa tsiku ndi tsiku.

Mwina siinu Mkhristu, mwinanso moyo sukukukomerani. Inunso mukhoza kumvera lamulo la Yesu. Bwerani kwa lye ndi kulandira moyo wake—umene uli wodzaza. Akunenanso kuti, “**Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wochuluka**” (Yohane 10:10b).

Anyamata otumikira ku ukwatiwo anamvera zonse zimene anawauza. Sanathire madzi a theka m'mitsukomo. Anadzaza “ndendende.” Kumvera Mulungu ndi mtima wanu wonse kumabweretsa chisangalalo ndi madalitso. “**Chilichonse mukachichita, gwirani ntchito mochokera mumtima, monga kwa Ambuye, osati kwa anthu ai; podziwa kuti mudzalandira kwa Ambuye mphotho ya cholowa; mutumikira Ambuye Khristu mwaukapolo**” (Akolose 3:23, 24).

Kodi zilipo zina zimene Yesu wakhala akukulankhulani kuti muzichite pomumvera lye? Bwanji osachita zimenezo lero?

Ophunzira ataona chozizwitsacho, chikhulupiriro chao chinakula—“Anamukhulupirira lye.” Mukamvera mau a Mulungu ndi kumuona Mulungu akugwira ntchito, chikhulupiriro chanu chidzakulanso. Chikhulupiriro chili ngati minyewa muthupi lathu. Imakhala yamphamvu *ikamagwiri-tsida* ntchito, popanga masewera kapena *kugwira* ntchito zolimbitsa thupi. Tiyen'i tisankhe kuyenda mwa chikhulupililo tsiku ndi tsiku. “**Koma munthu wolungama adzakhala ndi moyo ndi chikhulupiriro**” (Aroma 1:17b).

CHIKHULUPIRIRO ndicho kutaya zonse ndi kudalira lye.

PHUNZIRO 5. YESU AYERETSA KACHISI



Yohane 2:13-22

13Ndipo Paska wa Ayuda unayandikira, ndipo Yesu anakwera kunka ku Yerusalemu. **14**Ndipo anapeza m'Kachisi iwo akugulitsa ng'ombe ndi nkhosa ndi nkhunda, ndi akusinthana ndalamu aliku-khala pansi. **15**Ndipo pamene adapanga mkwapulo wazingwe, anatulutsa onse m'Kachisimo, ndi nkhosa ndi ng'ombe; nakhuthula ndalamu za osinhanawo, nagubuduza magome; **16**nati kwa iwo

akugulitsa nkhunda, Chotsani izi muno; musamayesa nyumba ya Atate wanga nyumba ya malonda. **17**Ophunzira ake anakumbukira kuti kunale-mbedwa, Changu cha pa nyumba yanu chandidya ine. **18**Chifukwa chake Ayuda anayankha nati kwa Iye, Mutinetsera ife chizindikiro chanji, pakuti muchita izi? **19**Yesu anayankha nati kwa iwo, Pasulani Kachisi uyu, ndipo masiku atatu ndidzamuutsa. **20**Pamenepo Ayuda anati, Zaka makumi anai ndi zisanu ndi chimodzi analimkumanga Kachisiyu, kodi inu mudzamuutsa masiku atatu? **21**Koma Iye analikunena za Kachisi wa thupi lake. **22**Chifukwa chake atauka kwa akufa, ophunzira ake anakumbukira kuti ananena ichi; ndipo anakulupirira cholemba, ndi mau amene Yesu ananena.

Zomwe Yesu adazidziwa

Kodi mukukumbukira tanthauzo la "Paska"? Tina-kambirana izi m'phunziro lina la m'mbuyomu. Yesu anapita ku Yerusalemukukakhala nao pa Paska. Zomwe anaziona mu kachisi sizidapereke chithunzi choti ndi malo opembedza Mulungu. Kapena malo oyanjanirana ndi Mulungu. Unali ngati msika wothinana! Nkhope ya Mulungu inali kutali nao. Izi Yesu anakwiya nazo.

Zoona zake zinali zakuti anthu sankagulitsa zifuyo ndi cholinga chakuti athu agwiritse ntchito popereka nsembe kwa Mulungu. Naonso ogulitsa ankakweza mitengo yao kwambiri motero kuti ankangowabera anthu. Ziwegoto anagulitsira mu kachisi mweni mweni! Sizodabwitsa kuti Yesu anawatulutsa mu kachisimo! Pa Marko 11:17b akunena kuti, **"Sichilembewa kodi, Nyumba yanga idzatchedwa nyumba yakupempheramo anthu a mitundu yonse? Koma inu mwaiyesa phanga la achifwamba."**

Yesu anauza atsogoleri Achiyuda mphamvu yake yoyeresa kachisi idzatsimikizika akadzaononga kachisi. Iye anati adzauka patatha masiku atatu! Anali odabwa chifukwa sankadziwa kuti Yesu ankanena za thupi lake. Yesu anadziwa kuti atsogoleri Achiyudawo ndiwo omwe adzamupachike. Anadziwanso kuti akadzatha masiku atatu atampachika, lye mwini adzaukitsa thupi lake kuchokera ku imfa.

Thupi la Yesu linali kachisi wa Mulungu

Zaka zambiri zidapita, kachisi yemwe Solomoni adama-nega "asanadzazidwe ndi ulemerero wa AMBUYE". Koma chifukwa chakuti mtundu wa Israele unali utatumikira milungu yonyenga, ulemerero wa Mulungu unachoka mu kachisimo ndipo kachisiyo anaonongedwa. Pambuyo pake kachisiyo anamangidwanso ndi iwo amene anafuna kubwerera-

nso kwa Mulungu nthawi imeneyo Mulungu anati, “... Ndi zofunika za amitundu onse zidzafika, ndipo ndidzadza-za nyumba iyi ndi ulemerero, ati Yehova wa makamu” (Hagai 2:7b). Pamenepa tikumuonanso Yesu, akubwera kudzayeretsa kachisi! Yesu ameneyo, kufika ponena kuti thupi lake ndi kachisi wa Mulungu!

“Pakuti mwa lye chikhalira chidzalo cha Umulungu m’thupi” (Akolose 2:9).

“... Mulungu ulemu nchachikulu...” (1 Timoteo 3:16).

“Onani namwali adzaima, nadzabala mwana wamwa-muna, ndipo adzamutcha dzina lake, Imanuele. Ndilo losandulika, Mulungu nafe” (Mateyu 1:23).

“Imene saidziwa mmodzi wa akulu a nthawi ya pansi pano: pakuti akadadziwa sakadapachika Mbuye wa ulemerero” (1 Akorinto 2:8). Kodi mukukumbukira momwe Yesu anayambira kuonetsera ulemerero wake mu phunziro 4? (Yohane 2:11) Atsogoleri achiyuda sanadziwe kuti Ambuye wa ulemerero anali pakati pao, anali mu thupi la Yesu ndipo anali nayo mphamvu yoyeretsa kachisi wake!

“Kodi simudziwa kuti muli Kachisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu?”
(1 Akorinto 3:16).

Kachisi wa Mulungu ali kuti lero?



Yesu amakhala mwa munthu aliyense amene wamulandira kwathunthu, kumulandira mumtima mwake kudzera mwa Mzimu Woyer! *Matupi athu ali kachisi wa Mulungu!* Maganizo apamwamba kwambiri! “**Kapena simudziwa kuti thupi lanu lili Kachisi wa Mzimu Woyer, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu? Ndipo simukhala a inu nokha. Pakuti munagulidwa ndi mtengo wake wapatali; chifukwa chake lemekezani Mulungu m'thupi lanu**” (1 Akorinto 6:19, 20).

Ndikofunika kwambiri kuti ife tidzikhala moyo woyer! Tisamachimwe ndi matupi athu, chifukwa chakuti ngati tinalandira Khristu m'moyo mwathu, ndife olumikizidwa naye ndipo tiyenera kukhala okhulupirika kwa lye. Mulungu ali ndi mphamvu yonse yotha kuyeretsa kachisi wake. Ali ndi mphamvu yonse yoyeretsa magawo onse a miyoyo yathu omwe sakumukondweretsa. Tiyeni tivomereze kuti atiyertse kudzera m'mau ake.

“Mnyamata adzayeretsa mayendedwe ake bwanji? Akawasamalira monga mwa mau anu” (Masalimo 119:9).

“**Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama lye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chili-chonse**” (1 Yohane 1:9).

“**Koma ngati tiyenda m'kuunika, monga lye ali m'kuunika, tiyanjana wina ndi mnzake, ndipo mwazi wa Yesu Mwana wake utisambitsa kutichotsera uchimo wonse**” (1 Yohane 1:7).

Mulungu samangopanga thupi la Mkhristu aliyense kukhala kachisi wake, komanso Akhristu onse amakhala “thupi la Khristu.” “**Chomwecho ife, ndife ambiri, tili thupi limodzi mwa Khristu**” (Aroma 12:5a). “**Ndipo lye ali mutu wa thupi, Mpingowo**” (Akolose 1:18a).

“Pali Khristu Yesu mwini, mwala wa pangodya; mwa lye chimango chonse cholumikizika pamodzi bwino, chikula, chikhale Kachisi wopatulika mwa Ambuye; chimene inunso mumangidwamo pamodzi, mukhale chokhalamo Mulungu mwa Mzimu” (Aefeso 2:20b-22). Munthu aliyense amene Mulungu amakhala mwa iye amakhala wamtengo wapatali! Tidzionetsetsa kuti tikuchitira zabwino Akhristu ena ndikuwaonetsera chikondi pakuti momwe tikuwachitira iwo, tikuchitiranso Khristu.

Tinene pamodzi ndi Paulo kuti, **“Tsopanonso Khristu adzakuzidwa m’thupi langa, kapena mwa moyo, kapena mwa imfa”** (Afilipi 1:20b).

Tiyeni tionetsetse kuti matupi athu omwe ali ndi kachisi wa Mulungu akhale malo opempherera, komwe timayankhula ndi Mulungu tsiku ndi tsiku ndipo nkhopre yake imakhala nafe. Matupi athu asakhale “phanga la akuba,” komwe zilako lako ndi zokoma zapadziko zimachotsa ulemerero wa Mulungu.

PHUNZIRO 6. YESU AFOTOKOZERA ZA KUBADWANSO MWATSOPANO

Yohane 3:1-8, 14-21, 36
¹Koma panali munthu wa Afarisi, dzina lake Nikodemo, mkulu wa Ayuda. ²Iyeyu ana-dza kwa Yesu usiku, nati kwa Iye, Rabi, tidziwa kuti Inu ndinu mphunzitsi wochokera kwa Mulungu; pakuti palibe

munthu akhoza kuchita zizindikiro zimene Inu muchita, ngati Mulungu sakhala na-ye. ³Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu.



⁴Nikodemo ananena kwa Iye, Munthu akhoza bwanji kubadwa atakalamba? Kodi akhoza kulowanso m'mimba ya amake ndi kubadwa? ⁵Yesu anayankha, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi Mzimu, sakhoza kulowa ufu-mu wa Mulungu. ⁶Chobadwa m'thupi chikhala thupi, ndipo chobadwa mwa Mzimu, chikhala mzimu. ⁷Usadabwe chifukwa ndinati kwa iwe, Uyenera kubadwa mwatsopano. ⁸Mphepo iomba pomwe ifuna, ndipo ukumva mau ake, koma sudziwa kumene ichokera, ndi kumene imuka; chotero ali-yense wobadwa mwa Mzimu.

¹⁴Ndipo monga Mose ana-

kweza njoka m'chipululu, chotero Mwana wa Munthu ayenera kukwezedwa; ¹⁵kuti yense wakukhulupirira akhale nao moyo wosatha mwa Iye.

¹⁶Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi koteru, kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakhu-lupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha.

¹⁷Pakuti Mulungu sanatumé Mwana wake kudziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi lika-pulumutsidwe ndi Iye.

¹⁸Wokhulupirira Iye saweruzidwa; wosakhulupirira waweruzidwa ngakhale tsopano, chifukwa sanakhulupirire dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. ¹⁹Koma chiweruziro ndi ichi, kuti kuunika kunadza kudziko lapansi, ndipo anthu anakonda mdima koposa kuunika; pakuti ntchito zao zinali zoipa. ²⁰Pakuti yense wakuchita zoipa adana nako kuunika, ndipo sakudza kwa kuunika, kuti zingatsutsidwe ntchito zake. ²¹Koma wochita

choonadi adza kukuunika,
kuti ntchito zake zionekere
kuti zinachitidwa mwa Mu-
lungu.

Mwanayo ali nao moyo
wosatha; koma iye amene
sakhulupirira Mwanayo sa-
dzaona moyo, koma mkwiyo
wa Mulungu ukhala pa iye.

³⁶Iye amene akhulupirira

Zoti muchite

A. Lembani mau oyenera kuchokera mu Phunziroli mu
mizere yosalembewamo.

1. Nikodemo anali _____ wa Ayuda (vesi 1).

Anadza kwa Yesu _____ (2).

[Yesu amakhudzidwa ndi munthu aliyense osauka
ngakhale olemera, ophunzira ngakhale osaphunzira.]

2. Nikodemo anaganiza kuti Yesu anali _____
wochokera kwa Mulungu (2).

3. Yesu anati, kuti munthu akaone ufumu wa Mulungu
ayenera ku_____ mwa_____ (3).

4. Munthu sangalowe ufumu wa Mulungu ngati sabadwa
mwa_____

ndi _____ .

[Malinga ndi momwe ankadziwira Nikodemo, madzi
ankatanthauza kuyeretsa. Muphunziro 2 tinaona kuti
Yohane M'batizi ankabatiza ndi madzi ndipo anthu
ankavomereza machimo ao ndi kulapa. Yesu anadza
kudzabatiza ndi Mzimu Woyeria ndi kuwapatsa anthu moyo
watsopano. Kuti tikalowe mu ufumu wa Mulungu, tiyenera
kukhala okonzekera kusiya machimo athu komanso
kulandira Mzimu wa Mulungu m'mitima yathu.]

5. Chobadwa mwathupi _____ (6).

[“Kuthupi” sizitanthauza matupi athu okha komanso zilakolako za umunthu zomwe zimakhala zodzikonda tokha (Aroma 8:8, 9).]

6. Icho chobadwa mwa Mzimu ndi _____ (6).

[Matupi athu akabadwa mwachilengedwe chathu (kuchokera kwa makolo athu a pansi pano) ifenso timakhala ndi matupi a pa pansi pano. Mizimu yathu ikakhala yobadwanso mwa Mulungu, ifenso timakhala ndi mzimu wamoyo, ndipo umakhala womvetsetsa ndi kuzindikira zinthu za uzimu za Mulungu (1 Akorinto 2:12, 14).]

7. Mwana wa munthu (Yesu) anayenera kukwezedwa (kupachikidwa pamtanda) monga _____ anakweza _____ mu chipululu (14).

8. Yesu anabwera chifukwa chakuti Mulungu _____ dziko lapansi. Yense wokhulupirira Yesu _____ koma adzakhala nawo _____ (16).

9. Mulungu sanatumize mwana wake kudziko lapansi kuti aka _____ dziko lapansi (ngakhale kuti adzaweruza dziko lapansi tsiku lina). Anatumiza mwana wake kuti dziko lapansi _____ (17).

10. Munthu amene amakhulupirira mwa Yesu sa _____ . Munthu amaweruzidwa pokhapokha ngati sa _____ mwa Yesu (18).

11. Kuunika kunadza padziko lapansi, ndipo anthu anakonda _____ koposa _____ chifukwa ntchito zao zinali _____ (19).

[Chiweruzo chimanthauza kuweruzidwa kwamuyaya komanso kulekanitsidwa ndi Mulungu.]

12. Yense wochita _____
amabwera kukuunika (21).

[Simunthu wochita zabwino yemwe amabwera poyer,
“Palibe mmodzi wakuchita zabwino, inde, palibe mmodzi ndithu” (Aroma 3:12b). Munthu wochita choonadi ndi yemwe amavomereza choonadi cha uchimo wake natsukidwa ndi Mulungu. **“Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama lye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse”** (1 Yohane 1:9).]

B. Mulembe mzere kunsi kwa mavesi opezeka mu phunziro 6 (Kapenanso mungolemba pa mapepala ang'ono ang'ono ndipo muloweze pamtima.)

Yohane 3:16 ndi Yohane 3:36

Kubadwanso mwatsopano kumanthauza chiyani?

Kubadwa kwatsopano ndiko kubadwa ndi “mphamuva zakumwamba” Kuyambanso moyo mwatsopano, kukhala ndi chiyambi *china*. Kubadwa mwa chilengedwe kumamupanga munthu kukhala chiwalo chimodzi cha mu banja lapansi pano. Kubadwa mumzimu kumamupanga munthu kukhala chiwalo cha m’banja la Mulungu. Mzimu umagwira ntchito mwa ife ndipo zikatero kusinthika kumaonekera kwa aliyense. Mwachitsanzo munthu amene anali wakuba, amasiya kuba. Ndi chimodzi modzi mphepo ikamaomba, sititha kuiwona mphepoyo, koma timaona ntchito zake.

Munthu amene mzimu wake si wobadwanso mwa Mulu-

ngu, amakhala "wakufa" muuzimu (Aefeso 2:1, 5). Kutsukidwa ku machimo kumabwera choyamba ndi imfa ya chikhristu, ndi kufa kwa ife eni kuntchito zathu zakale. Zikatero mzimu umatipatsa moyo watsopano—woukitsidwa ndi Khristu zonsezi ndi zofunikira polowa ufumu wa Mulungu. Kubadwa kwatsopano kumachitika pamene Mzimu Woyeram (mzimu wake wa Yesu Khristu) akalowa ndikukhala mwa ife, "**Koma ngati munthu alibe Mzimu wa Khristu, siali wake wa Khristu**" (Aroma 8:9b).

Timatengera chilengedwe cha Khristu (2 Petro 1:4): maganizo atsopano, chilimbikitso cha ntchito zathu, maganizo atsopano pa kamvetsedwe ka malembo oyera.

Kodi inu muli ngati Nikodemo? Mwina ndinu munthu wopembedza kuyambira kale. Kapenanso munthu amene mumamvera malamulo onse. Mwinanso ndinu mtsogoleri. Kodi mudayamba mwabadwa mwatsopano ndi mphamvu ya Mzimu Woyerwa wa Mulungu? Kuti mukhale olengedwa mwatsopano? "**Chifukwa chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano**" (2 Akorinto 5:17). "Ngati simunabadwenso kwatsopano," bwanji osabwera kwa Yesu lero, ngati m'mene anachitira Nikodemo? Mupempheni Yesu kuti alowe mumtima mwanu, kuti mukhale nawo moyo watsopano ndikukhala m'banja la Mulungu. "**Iye wakukhala ndi Mwana ali nao moyo; wosakhala ndi Mwana wa Mulungu alibe moyo**" (1 Yohane 5:12).

Mose m'chipululu

Kalekale ana a Israele anali m'chipululu pansi pa utsogoleri wa Mose ndipo iwo anayankhula zonyoza



Mulungu ndi Mose. Amadandaula chifukwa cha momwe Mulungu ankakwanirtsira zosowa zao. Chifukwa cha ichi, Mulungu anatumiza njoka kuti zikawalume ndipo anthu ambiri anafa. Anthu anabwera kwa Mose kudzavomereza machimo ao. Anamupempha Mose kuti awapempherere kuti Mulungu achotse njoka zomwe zinali pakati pao. Mulungu anayankha pemphero lao mu njira yosiyanasiyana. Mulungu anamuua Mose kuti apange njoka ya mkuwa ndi kuikweza pamtengo. Yense oyang'ana pa njoka ya nkuwayo ngakhale atalumidwa ndi njoka yoopsayo akangoyang'ana adzakhala ndi moyo. (Nkhani imeneyi ikupezeka pa Numeri 21:4-9.)

Tchimo lili ngati ululu wa njoka yoopsa. Ifenso tidzafa ngati sitiyang'ana kwa Yesu, yemwe anakhala ngati wochimwa chifukwa cha ife (ngakhale kuti lye sanachimwe). Anathera mu chipululu. Okhawo amene anayang'ana pa njoka ya mkuwa anakhala ndi moyo. Yesu anamuchenjeza Nikodemo kuti iyenso adzafa ngati sayang'ana kwa Yesu ndi kulandira moyo watsopano.

Monga anthu anayang'ana njoka "yakufayo" nakhala ndi moyo, iwonso ayenera kuyang'ana lye amene achotsa tchimo la dziko lapansi, kudzera pa imfa yake ya pamtanda, (Yohane 12:32, 33). Yang'anani ndipo mukhale ndi moyo! Sanasowe kumvetsetsa kuti adakachira "bwanji" akayang'ana njoka yamkuwa. Iwo ankangoyenera kumvera mwa chikhulupiriro. Ndipo zinkatheka!

**Yang'ana m'bale wanga!
Kwa Yesu kuli moyo;
Kwalembedwa m'mau ake Halleluya!
"Yang'ana ukhale ndi moyo."**

Kutsatira kuunika

Tikabwera kwa Khristu, tchimo lathu limaonekera chifukwa Yesu ndiye kuunika kweni kweni (Yohane 1:9). Mdima umabisa choonadi, koma kuunika kumaunikira monga momwe zinthu zilili.

Iye wokana kutsatira kuunika kwa Mulungu akusankha kukakamira tchimo ndi kukananso kuti Mulungu amusinthe. Munthu wochimwa ulendo wake ndi wa ku Gehena. Kuti apulumuke chionongeko akusowa Khristu. Anthu omwe alibe Yesu ali pansi pa mkwiyo wa Mulungu (Yohane 3:36). Koma iye wolandira Khristu ndiye wayamba umoyo umene ukakhale nao kumwamba—moyo wosatha wa Mulungu. **"Ndipo uwu ndi uthenga tidaumva kwa lye, ndipo tiulalikira kwa inu, kuti Mulungu ndiye kuunika, ndipo mwa lye monse mulibe mdima. Tikati kuti tiyanjana ndi lye, ndipo tiyenda mumdima, tinama, ndipo sitichita choonadi; koma ngati tiyenda m'kuunika, monga lye ali m'kuunika, tiyanjana wina ndi mnzake, ndipo mwazi wa Yesu Mwana wake utisambitsa kutichotsera uchimo wonse"** (1 Yohane 1:5-7).

Munthu akafuna kukhala moyo woyerwa, akhale wokonzeka kuonetsa machimo ako poyerwa ndikukhululukidwa. Chifukwa cha ichi, kubwera kwa Yesu ndiko kutsatira moyo komanso imfa. Tsgolo lanu litengera pa zomwe mu-kuchita ndi nyali yanu. Kodi mu-kuitsatira, kapena mukuithawa?





**CHIKHULUPIRIRO +MAU A MULUNGU (YESU) =
MOYO WOSATHA**

PHUNZIRO 7. YESU APEREKA MADZI OPATSA MOYO

mwana wake Yosefe; ⁶ndipo pamenepo panali chitsime cha Yakobo. Ndipo Yesu, popeza analema ndi ulendo wake, motero anakhala ndi ulendo wake, motero anakhala pachitsime. ⁷Kunali ngati ora lachisanu ndi chimodzi. Kunadza mkazi wotuluka m'Samariya kudzatunga madzi. Yesu ananena naye, Undipatse Ine ndimwe. ⁸Pakuti ophunzira ake adachoka kunka kumudzi kuti akagule chakudya. ⁹Pamenepo mkazi

Yohane 4:5-42

5Chifukwa chake anadza kumudzi wa Samariya, dzina lake Sikari, pafupi pa kadziko kamene Yakobo adapatsa

wa m'Samariya ananena ndi Iye, Bwanji Inu, muli Myuda, mupempha kwa ine kumwa, ndine mkazi Msamariya? (Pakuti Ayuda sayenderana nao Asamariya). ¹⁰Yesu anayankha nati kwa iye, Ukadadziwa mtulo wa Mulungu, ndi Iye amene alinkunena ndi iwe, Undipatse Ine ndimwe; ukadapempha Iye, ndipo akadakupatsa madzi amoyo. ¹¹Mkaziyo ananena ndi Iye, Ambuye, mulibe chotungira madzi, ndi chitsime chili chakuya; ndipo mwatenga kuti madzi amoyo? ¹²Kodi muli wamkulu ndi atate wathu Yakobo amene anatipatsa ife chitsimechi, namwamo iye yekha, ndi ana ake, ndi zoweta zake? ¹³Yesu anayankha nati kwa iye, Yense wakumwako madzi awa adzamvanso ludzu; ¹⁴koma iye wakumwa madzi amene Ine ndidzampatsa sadzamva ludzu nthawi zonse; koma madzi amene Ine ndidzampatsa adzakhala mwa iye kasupe wa madzi otumphukira kumoyo wosatha.

¹⁵Mkaziyo ananena kwa Iye, Ambuye, ndipatseni ma-

dzi amene, kuti ndisamve ludzu, kapena ndisadze kuno kudzatunga. ¹⁶Yesu ananena kwa iye, Muka, kamuitane mwamuna wako, nudze kuno. ¹⁷Mkazi anayankha nati kwa Iye, Ndilibe mwamuna. Yesu ananena naye, Wanena bwinno, kuti mwamuna ndilibe; ¹⁸pakuti wakhala nao amuna asanu; ndipo iye amene ukhala naye tsopano sali mwamuna wako; ichi wanena zonna. ¹⁹Mkazi ananena ndi Iye, Ambuye, ndizindikira kuti muli Mneneri. ²⁰Makolo athu analambira m'phiri ili; ndipo inu munena, kuti m'Yerusalemu muli malo oyenera kulumbiramo anthu. ²¹Yesu ananena naye, Tamvera Ine, mkazi iwe, kuti ikudza nthawi, imene simudzalambira Atate kapena m'phiri ili, kapena m'Yerusalemu. ²²Inu mulambira chimene simuchidziwa; ife tilambira chimene tichidziwa; pakuti chipulumutso chichokera kwa Ayuda. ²³Koma ikudza nthawi, ndipo tsopano ilipo, imene olambira oona adzalambira Atate mumzimu ndi m'choonadi; pakuti Atate

afuna otere akhale olambira ake.²⁴Mulungu ndiyemzimu; ndipo omlambira Iye ayenera kumlambira mumzimu ndi m'choonadi.²⁵Mkazi ananena ndi Iye, Ndidiwa kuti Mesiya adza (wotchedwa Khristu): akadzadza Iyeyu, adzatiuza zonse.²⁶Yesu ananena naye, Ine wakulankhula nawe ndine amene.

²⁷Ndipo pamenepo anadza ophunzira ake; nazizwa kuti analinkulankhula ndi mkazi; koma panalibe wina anati, Mufuna chiyani? Kapena, mulankhula naye chiyani?²⁸Pamenepo mkazi anasiya mtsuko wake, namuka kumudzi, nanena ndi anthu,²⁹Tiyeni, mukaone munthu, amene anandiuzazinthu zilizonse ndinazichita: ameneyu sali Khristu nanga?³⁰Anatuluka iwo m'mudzi ndipo analinkudza kwa Iye.

³¹Pa mphindikati iyio phunzira ake anampempha Iye, ndi kunena, Rabi, idyani.

³²Koma Iye anati kwa iwo, Ine ndili nacho chakudya chimene inu simuchidziwa.

³³Chifukwa chake ophunzira

ananena wina ndi mnzake, Kodi pali wina anamtengera Iye kanthu kakudya?³⁴Yesu ananena nao, Chakudya changa ndicho kuti ndichite chifuniro cha Iye amene anandituma Ine, ndi kutsiriza ntchito yake.³⁵Kodi simunena inu, kuti, Yatsala miyezi inai, ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu, Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta.³⁶Wakumweta alandira kulipira, na sonkhanitsira chobala kumoyo wosatha; kuti wofesayo akakondwere pamodzi ndi womwetayo.³⁷Pakuti m'menemo chonenacho chili choona, Wofesa ndi wina, womweta ndi winanso.³⁸Ine ndinatuma inu kukamweta



chimene simunagwirirapo ntchito: ena anagwira ntchito, ndipo inu mwalowa ntchito yao.

³⁹Ndipo m'mudzi muja anthu Asamariya ambiri anamkhulupirira Iye chifukwa cha mau a mkazi, wochita umboniyo, kuti, Anandiua ine zinthu zilizonse ndinazicha. ⁴⁰Chifukwa chake pamene Asamariya anadza kwa

Iye, anamfunsa akhale nao; ndipo anakhala komweko masiku awiri. ⁴¹Ndipo ambiri oposa anakhulupirira chifukwa cha mau ake; ⁴²ndipo ananena kwa mkazi, kuti, Tsopano sitikhulupirira chifukwa cha kulankhula kwako: pakuti tamva tokha, ndipo tidziwa kuti Mplumutsi wa dziko lapansi ndi Iyeu ndithu.

Zoti muchite

A. Yankhani mafunso kuchokera ku phunziroli.

1. Yesu ankamva chiyani zomwe zikutitsimikizira kuti analidi ndi thupi la umunthu? _____

(vesi 6)

2. Yesu anamuuza chiyani mkazi wa ku Samariya?
_____ (7)

3. Chifukwa chiyani anadabwa Yesu akuyankhula naye?
(9) _____

[Asamariya anali anthu obadwa kuchokera kwa Ayuda ndi anthu ena obwera omwe Ayuda ankakwatirana nawo. Pambali popembedza Mulungu woona wa Israele iwo amapembedzanso milungu ina yonyenga. Ayuda atamanganso kachisi wao ku Yerusalem, sanalole kuti Asamariya awathandize ntchitoyo. Koma Yesu ankakonda

munthu aliyense payekha, ankakwanirtsa ngakhale zosowa za wina aliyense ngakhale kuti ichi sichinali chikhaldwe cha Ayuda kuti munthu wamamuna nkuyankhulana ndi munthu wamkazi pagulu.]

4. Mzimaiyu akadadziwa choyenera kupempha, Yesu akadampatsa chiyani? (10) _____

5. Kodi pakadakhala kusiyana kotani pakati pa kumwa madzi a pachitsime ndi kumwa madzi amene Yesu akadampatsa? (13, 14) _____

6. Yesu adadziwa chiyani za mzimayi uyu? (18)

[Yesu amadziwa machimo obisika a *aliyense wa ife*.]

7. Yesu atamuza mzimaiyo machimo ake, mzimaiyo anayamba kunena nkhani yanji? (vesi 20) Ananena za malo amene anthu anayenera ku _____

[Asamariya ankapembedwa mu kachisi wa kuphiri la Gerizimu. Ankakhulupirira mu mabuku asanu oyamba okha m'Chipangano Chakale. Kodi mumakonda kukambirana za "chipembedzo" m'malo molungamitsidwa ndi Mulungu?]

8. Opembedza mu choonadi amapembedza Mulungu motani? (23) _____

[Pofuna kupembedza Mulungu moona, tiyenera kubadwa mwa Mzimu.]

9. Mzimaiyo atamuzindikira Yesu anachita chiyani? (28, 29) _____

10. Chinamukhutitsa Yesu ngati chakudya ndi chiyani? (34)

11. Asamariya ankakhulupirira kuti Yesu anali ndani? (42)

B. Lowezani vesi ili: **Yohane 4:24**

Chikhulupiro chimakula bwanji

Kodi sizosangalatsa kuona m'mene mzimai wa ku Samariya anamudziwira ndi kumukhulupirira lye pomwe Yesu anapitirira kuyankhula naye? **Taonani vesi 9.** Poyamba akumuzindikira Yesu ngati Myuda yemwe wayankhula naye mwa chifundo. **Taonani vesi 11.** Ulemu wake ukukulilakulirabe ndipo akumutchula kuti "Ambuye." **Taonani vesi 19.** Yesi anadziwa zambiri za iye kotero kuti mzimaiyo anayamba kuganiza kuti Yesu anali mneneri. **Taonani vesi 29.** Tsopano anayamba kukhulupirira kuti Yesu anali Mesiya wlonjezedwa.

Tikavomera kuti Yesu ayankhule nafe kudzera mu Baibulo, chikhulupiro chathu chimakulanso kwambiri. "**Chomwecho chikhulupiro chidza ndi mbiri, ndi mbiri idza mwa mau a Khristu**" (Aroma 10:17).

Madzi amoyo ndi chiyani?

Mzimai wa ku Samariya anaganiza kuti chikadakhala chinthu chabwino atatsitsira mtsuko wake mu chitsime cha Yakobo kuti atunge madzi. Chitsimecho chinali chozama kwambiri ndipo pamene panali madzi kuya kwake kunali ngati mamita okwanira 30. Koma Yesu sikuti ankanena madzi omwe timamwa. Yesu ankanena za kuhutitsidwa koma akadampatsa mzimaiyo kuti asiye kumva ludzu la

uzimu lomwe linkamupangitsa kukhala ndi zilakolako za uchimo. *Madzi amoyo* ndiwo mphatso ya moyo wosatha, moyo wa lye mwini. Kasupe *wotumphukira* ku moyo wa chimwemwe ndi mtendere tikhaza kukhala naye ngati t-dzazidwa ndi Mzimu Woyeria!

Maiyo akufuna madzi koma Yesu akufuna kumukumbutsa zina. Ayenera *kuvomera* machimo aka ndi kuvomereza kutembenuka ndi kuwasiya asanamupatse madzi a moyo.

Phunziroli likutiua chiyani pa za kutumikira Mulungu

1. Munthu *aliyense* ayenera kumva uthenga wabwino ndi kukhulupirira Khristu kuti apulumutsidwe. Tisawanyoze anthu ngati kuti iwo ndi akunja kapena osavomerezeka chifukwa Yesu sanachite choncho.

2. "Minda" ya uzimu pa dziko lapansi ili ndi zipatso zaku-cha komanso zokhwima ndipo ziyenera kukololedwa. Ti-kweze maso ndi kuona chiwerengero cha anthu omwe ali ndi njala ya chilungamo ndipo ali okonzeka kuchilandira.

3. Munthu m'modzi akhoza kufesa (kuuza ena za Yesu, kupereka kwa anthu zinthu zowerenga ndi kuwaphunzitsa mau a Mulungu). Munthu wina akhoza kukolola (kumubweretsa munthu wina kuti adziwanene ndi Khristu). Tiyenera kukhala okonzeka kuchita chimodzi mwa zinthu ziwirizi. Anthu awiri onsewa, ofesa *ndi* okolola akhoza kukhala ndi chimwemwe.

4. Kuchita chifuniro cha Mulungu ndi *kumaliza* nchito ya-thu tsiku ndi tsiku kumabweretsa kukhutitsidwa koposa ngakhale chakudya chimene timadya.

5. Ngakhale kuli kofunika *kuuza* anzathu ena za Yesu, tiyeneranso *kuwabweretsa* kwa lye kuti *adziwane* naye.

PHUNZIRO 8. YESU ACHIRITSA MWANA WA NDUNA YAMFUMU



Yohane 4:46-53

46Chifukwa chake Yesu anadzano ku Kana wa m'Galileya, kumene anasandutsa madzi vinyo. Ndipo kunali mkulu wina wa mfumu, mwana wake anadwala m'Kaperao. **47**Iyeyu, pamene anamva kuti Yesu wachokera ku Yudeya nafika ku Galileya, ananka kwa Iye, nampempha kuti atsike kukachiritsa mwana wake; pakuti anali pafupi imfa. **48**Pamenepo Yesu anati kwa iye, Ngati simuona zizi-

ndikiro ndi zozizwa, simudza-khulupirira. **49**Mkuluyo ana-nena kwa Iye, Ambuye, tsi-kani asanafe mwana wanga. **50**Yesu ananena naye, Muka, mwana wako ali ndi moyo. Munthuyu anakhulupirira mau amene Yesu anatero naye, namuka. **51**Ndipo m'me-ne analikutsika, akapolo ake anakomana naye, nanena, kuti, Mwana wanu ali ndi moyo. **52**Chifukwa chake anawafunsa ora lake anayamba kuchi-ralo. Pamenepo anati kwa iye, kuti, Dzulo, ora lachisanu ndi chiwiri malungo anamsiya. **53**Chifukwa chake atateyo anadziwa kuti ndi ora lomwe-lo limene Yesu anati kwa iye, Mwana wako ali ndi moyo; ndipo anakhulupirira iye yekha ndi a pa banja lake onse.

Mphamvu yopezeka mu mau a Mulungu

Mulungu akanena kanthu kamachitika! Mulungu amene analenga dziko lapansi ndi lakumwamba ndi zonse zokhalamo pongolankhula mau ndi amene tikumuona

akulankhula ndi nduna ya mfumu kuti, "Muka, mwana wako ali ndi moyo" (Yohane 4:50) ndipo zinakhaladi chomwecho.

Yesu anati zonse zolonjezedwa mu Baibulo (Mateyu 5:18). Kodi inu mumakhulupirira mau a Mulungu? Zochita zanu zimaonetsa kuti mumakhulupirira—ngati m'mene tikumuonera munthu wa mu nkhaniyi?

Mau athu ali nayo mphamvu. Izi zingachitike *ngati Khristu ali m'mitima yathu*. Mu Marko 11:22, 23 Yesu anauza ophunzira ake kuti, "**Ndipo Yesu anayankha nanena nao, Khulupirirani Mulungu. Ndithu ndinena ndi inu, kuti, Munthu aliyense akanena ndi phiri ili, Tanyamulidwa, nuponyedwe m'nyanja; wosakayika mumtima mwake, koma adzakhulupirira kuti chimene achinena chichitidwa, adzakhala nacho.**" Mau amene timayankhula akanelledwa mwa chikhulupiro mwa Mulungu amakhala ndi *mphamvu*. Mumayankhula mau otani? Mumayankhula zolimbikitsa, kutonthoza, kukhulupirira ndi chikondi?

Phunziroli likutiphunzitsa chiyani za pemphero

Kodi Yesu amayankha mapemphero athu masiku ano? Ahebri 13:8 akutiuba kuti "**Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, ndi lero, ndi kunthawi zonse.**" Timadziwa kuti ndife oyenera kubwera kwa lye ndi zopempha zathu. lye amatiuba kuti, "**Ndipo wakudza kwa Ine sindidzamtaya iye kunja**" (Yohane 6:37b). Amatiuba kuti, "**Pemphani, ndipo chidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo chidzatsegulidwa kwa inu**" (Mateyu 7:7).

Komanso tikhulupire kuti atiyankha. "**Koma wopanda chikhulupiro sikutheka kumkondweretsa; pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti alipo, ndi kuti ali wobwezera mphotho iwo akumfuna lye**" (Ahebri 11:6).

Tiyenera kukhutitsidwa ndi yankho lomwe Yesu amapereka, Nduna ya mfumu inampempha Yesu kuti apite naye ku nyumba kwake, koma Yesu sanatero; m'malo mwake anati, **"Muka, mwana wako ali ndi moyo"** (Yohane 4:50). Mwina sangakuyankheni monga mwa pemphero lanu, komabe amachita mokomera inu, molingananso ndi mau ake!

Chikhulupiriro sichibweretsa *chiwombolo* nthawi zonse. (Muone mau opezeka pa Ahebri 11:35-39). Koma chikhulupiliro nthawi zonse chimabweretsa mtendere, ndi *chitsogozo*. **"Musadere nkhawa konse; komatu m'zonse ndi pemphero, ndi pembedzero, pamodzi ndi chiyamiko, zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu. Ndipo mtendere wa Mulungu wakupambana chidziwitso chonse, udzasunga mitima yanu ndi maganizo anu mwa Khristu Yesu"** (Afilipi 4:6, 7).

Mukakhulupirira Mulungu, ndipo Mulungu amagwira ntchito ndi mphamu, chikhulupiriro chanu chidzalimbikitsidwa. Chikhulupiriro cha *banja lanu* chidzalimbikitsidwano, ngati momwe zinakhalira ndi banja la nduna ya mfumu *banja lonse* la nduna ya mfumu linakhulupirira Mulungu.

PHUNZIRO 9. YESU ACHIRITSA MUNTHU PA THAMANDA LA BETESIDA

Yohane 5:1-9, 14-18

¹Zitapita izi panali chikondwerero cha Ayuda; ndipo Yesu anakwera kunka ku Yerusalemu. ²Koma pali tha-

mande m'Yerusalemu pa Chipata cha Nkhosa, lotchedwa m'Chihebri Betesida, lili ndi makonde asanu. ³M'menemo munagona khamu lalikulu la



anthu odwala, akhungu, opunduka miyendo, opuwala. Mabuku ena akale amaonjezerapo. ⁴Nthawi zina mngelo wa Ambuye ankatsikira pa thamandaloo navundula madziwo. Woyamba kuluwamo madzi atavundulidwa, anachiritsidwa nthenda iliyonse imene anali nayo. ⁵Koma panali munthu wina apo, ali m'kudwala kwake zaka makumi atatu kudza zisanu ndizitatu. ⁶Yesu, pakuona ameneyo alikugona, ndipo anadziva kuti anatero nthawi yaikulu pamenepe, ananena naye, Ufuna kuchiritsidwa kodi? ⁷Wodwalayo anayankha, Ambuye, ndilibe wondiviika

ine m'thamanda, paliponse madzi avundulidwa; koma m'mene ndilinkudza ine, wina atsika ndisanatsike ine. ⁸Yesu ananena naye, Tauka, yalula mphasa yako, nuyende. ⁹Ndipo pomwepo munthuyu anachira, nayalula mphasa yake, nayenda. Koma tsiku lomwelo linali la Sabata.

¹⁴Zitapita izi Yesu anampeza m'Kachisi, nati kwa iye, Taona, wachiritsidwa; usachimwenso, kuti chingakugwere choipa choposa. ¹⁵Munthuyo anachoka, nauza Ayuda, kuti ndiye Yesu amene adamchiritsa. ¹⁶Ndipo chifukwa cha ichi Ayuda analondalonda Yesu, popeza anachita izo tsiku la Sabata.

¹⁷Koma Yesu anayankha iwo, Atate wanga amagwira ntchito kufikira tsopano, Inenso ndigwira ntchito. ¹⁸Chifukwa cha ichi Ayuda anaonjeza kufuna kumupha, si chifukwa cha kuswa tsiku la Sabata kokha, komatu amatchanso Mulungu Atate wake wa Iye yekha; nadziyesera wolingana ndi Mulungu.

Zoti muchite

Mulembe mau oyenera m'mizere mosalembedwamo.

1. Munthu wina ankayembekezera pa thamanda la Betesida. Anadwala ndipo anali ofooka kwa zaka (vesi 5).

2. Yesu anamufunsa funso lofunikira kwambiri, "Kodi uku-funa _____?" (6)

3. Yesu anamuuzza kuti achite zomwe zimaoneka ngati zosatheka. Anati " _____ yalula mphasa yako _____" (8).

4. Pambuyo pake Yesu atamupeza mu kachisi anati, "Taona wachiritsidwa _____ kuti chingakugwere choipa choposa" (14).

5. Ayuda ankafuna kumupha Yesu pa zifukwa ziwiri: (a) chifukwa cha _____ (18)

[pochiritsa munthu tsiku limene Ayuda sanayenera kugwira ntchito ili yonse], (b) chifukwanso chonena kuti Mulungu anali atate wake _____ (18).

Ukufuna kuchiritsidwa kodi

Mwina mukusowa kuchiritsidwa ndi kulimbikitsidwa mu thupi, maganizo ndi malingaliro *anu?* Mwina muli ndi chizolowezi choipa chomwe chimakulepheletsani kutumiki-ri Mulungu momwe mufunira. Kabenango mkwiyo ndi kuwawidwa mumtima ndi zimene zimakuvutani kwambiri.

Yesu akuona chosowa chanu ndipo akukufunsani kuti, “**Ukufuna kuchiritsidwa kodi?**” Mukhoza kukhala nako kuwiringula pofotokoza zifukwa zomwe zikukupangitsani kuti mudzivutika. Mwina m’banja mwanu kapena ku sukulu kwanu mkhristu ndi inu nokha. Kabenanso mavuto omwe amakuchitikirani ndiwo akupangitsa kuti zinthu zisokonekere. Koma izi sizingamuvute Yesu. Akhoza kukuchiritsani *tsopano lino!* Koma mwina akhoza kukufunsani kuti muchite zomwe zingaoneke ngati zosatheka. Monga momwe anamufunsira munthu amene ankalephera kuyenda namuuza kuti ayimirire ndipo ayende komanso ayalule mphasa yake. Chilichonse chomwe chingakhalepo, pamene *mwayamba* kumvera mau a Mulungu, Yesu adzakupatsani mphamvu zomwe mukuzisowa ndipo adza-kuchiritsani. Ndipo adzakupatsani moyo wa chigonjetso.

PHUNZIRO 10. ZIUKITSO ZIWIRI

Yohane 5:24-29

²⁴Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti iye wakumva mau anga, ndi kukhulupirira Iye amene anandituma Ine, ali nao moyo wosatha, ndipo salowa m’kuweruza, koma wachokera kuimfa, nalowa m’moyo. ²⁵Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti ikudza nthawi, ndipo ilipo *tsopano*,

imene akufa adzamva mau a Mulungu; ndipo iwo akumva adzakhala ndi moyo. ²⁶Pakuti monga Atate ali ndi moyo mwa Iye yekha, momwemo-nso anapatsa kwa Mwana kukhala ndi moyo mwa Iye yekha; ²⁷ndipo anampatsa Iye mphamvu ya kuchita mlandu, pakuti ali Mwana wa Mu-

nthu. ²⁸Musazizwe ndi ichi, amene adachita zabwino,
kuti ikudza nthawi, imene kukuuka kwa moyo; koma
onse ali m'manda adzamva amene adachita zoipa kukuu-
mau ake, ²⁹nadzatulukir a, ka kwa kuweruza.

Taganizirani izi

Kodi sichinthu cha mtengo wapatali pamene tikumva Yesu akugogoda pakhomu la mitima yathu kuti ife timukhulupirire ndikumtsegulira kuti alowe. Imeneyo ndiyo *nthawi imene timakhala ndi chikhulupiro chakuti tili nawo moyo wosatha!* *Timadziwa* kuti sitidzatsutsidwa. Tidzazindikira kuti *tadutsa* kuchokera ku imfa kulowa moyo. Kodi mumadabwa kuti zimenezi zingatheke bwanji? Ichi ndi chifukwa chakuti Yesu ali ndi *moyo mwa lye yekha* (vesi 26). *Iwo amene alibe Khristu sangathe kumukondweretsa Mulungu* (Aroma 8:8) chifukwa cha ichi pamene awukitsidwa kumanda, amangoyembekezera chiweruzo komanso kulekanitsidwa ndi Mulungu ku nthawi za nthawi.

Zoti muchite

Muloweze pamtima Yohane 5:24 ngati chitsimikizo cho-kukumbutsani tanthauzo la chipulumutso chanu. Pokhapo-kha ngati mukumva Mau a Mulungu ndi kukhulupirira lye (kumvera lye kumaonetsa kuti mukumukhulupirira) musalole Satana kuti ayike chikaiko m'maganizo mwanu. Mulungu akufuna *mudziwe* kuti ndinu anthu ake. China chikabwera pakati pa inu ndi Mulungu, Mulungu akufuna kukuunikirani kuti muvomereze ndi kuchichotsa. Mulungu *amabwezeretsa*. Satana kwake *nkutitsutsa* kuti *ndife olakwa*.

PHUNZIRO 11. YESU NDI MKATE WA MOYO

Yohane 6:5-14, 35, 47-51, 53-56, 63

⁵Pamenepo Yesu, pokweza maso ake, ndi kuona kuti khamu lalikulu lilinkudza kwa Iye, ananena kwa Filipo, Tidzagula kuti mikate kuti adye awa? ⁶Koma ananena ichi kuti amuyese; pakuti anadziza wa yekha chimene adzachita. ⁷Filipo anayankha Iye, Mikate ya marupiya atheka mazana awiri siikwanira iwo, kuti yense atenge pang'ono. ⁸Mmodzi wa ophunzira ake, Andrea, mbale wake wa Simoni Petro, ananena ndi Iye, ⁹Pali mnymata pano, amene ali nayo mikate isanu yabarele, ndi tinsomba tiwiri; koma nanga izi zifikira bwanji ambiri otete? ¹⁰Nati Yesu, Akhalitseni anthu pansi. Ndipo panali udzu wambiri pamalopo. Pamene po amunawo anakhala pansi, kuwerenga kwao monga zikwi zisanu. ¹¹Pomwepo Yesu antenga mikateyo; ndipo pame ne adayamika, anagawira iwo akukhala pansi; momwemo nso ndi tinsomba, monga momwe iwo anafuna. ¹²Ndipo pa-

mene adakhuta, Iye ananena kwa ophunzira ake, Sonkhanitsani makombo kuti kasatayike kanthu. ¹³Pomwepo anasonkhanitsa, nadzaza madengu khumi ndi awiri ndi makombo a mikate isanuyo yabarele, amene anatsalira anadyawo. ¹⁴Chifukwa chake, anthu, poona chizindikiro chimene anachita, ananena, kuti, Ameneyo ndiye mneneri ndithu wakudzayo m'dzikolo lapanisi.

³⁵Yesu anati kwa iwo, Ine ndine mkate wamoyo; iye amene adza kwa Ine sadzamva njala, ndi iye amene



akhulupirira Ine sadzamva ludzu nthawi zonse.

⁴⁷Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Iye wokhulupirira ali nao moyo wosatha. ⁴⁸Ine ndine mkate wamoyo. ⁴⁹Makolo anu adadya m'chipululu, ndipo adamwalira. ⁵⁰Mkate wotsika Kumwamba ndi uwu, kuti munthu akadyeko ndi kusamwalira. ⁵¹Mkate wamoyo wotsika Kumwamba Ndine amene. Ngati munthu wina akadyako mkate umene, adzakhala ndi moyo kosatha. Inde, ndipo mkate umene ndi-dzapatsa Ine, ndiwo thupi langa, ukhale moyo wa dziko lapansi.

⁵³Chifukwa chake Yesu ana-

ti kwa iwo, Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Ngati si-mukudya thupi la Mwana wa Munthu ndi kumwa mwazi wake, mulibe moyo mwa inu nokha. ⁵⁴Iye wakudya thupi langa ndi kumwa mwazi wa-naga ali nao moyo wosatha; ndipo Ine ndidzamuukitsa iye tsiku lomaliza. ⁵⁵Pakuti thupi langa ndi chakudya ndithu, ndi mwazi wanga ndi chaku-mwa ndithu. ⁵⁶Iye wakudya thupi langa ndi kumwa mwazi wanga akhala mwa Ine ndi Ine mwa iye.

⁶³Wopatsa moyo ndi mzi-mu; thupi silithandiza konse. Mau amene ndalankhula ndi inu ndiwo mzimu, ndi moyo.

Zoti muchite

Muloweze pamtima mau awa: **Yohane 6:35** ndi **Yohane 6:63**

Zomwe phunziroli likutiphunzitsa

1. Yesu amasamalira zosowa zathu. Ali ndi chikonzero chofuna kukwaniritsa zosowa zathu zonse, koma akufuna kuchiyesa chikhulupiro chathu mwa lye. Akufuna tidziyang'ana kwa lye ndi *kumdalira* pa chosowa chathu chiri chonse.

2. Ngakhalenso Yesu anathokoza chifukwa cha *zochepa* zimene anali nazo. Mulungu akutiuzza kuti, "**M'zonse**

yamikani; pakuti ichi ndi chifuniro cha Mulungu cha kwa inu, mwa Khristu Yesu” (1 Atesalonika 5:18).

3. Yesu akhoza kuthetsa vuto lililonse monga mwa *kuchuluka* kwake. “**Ndipo kwa lye amene angathe kuchita koposaposatu zonse zimene tizipempha, kapena tiziganya, monga mwa mphamvu ya kuchita mwa ife**” (Aefeso 3:20).

4. Mulungu sakondwera ndi kusakaza. lye amafuna kuti tigwiritse ntchito *chilichonse* chimene watipatsa, “kuti pasatayikepo kanthu.”

Akufuna tidzigwiritse ntchito bwino *nthawi* yathu. “**Akuchita machawi, popeza masiku ali oipa. Chifukwa chake musakhale opusa, koma dziwitsani chifuniro cha Ambuye nchiyani**” (Aefeso 5:16, 17).

Akufuna tigwiritse bwino ntchito *mphatso* ndi *kuthekera* kwathu mwa nzeru: “**Mbuye wake anati kwa iye, Chabwino, kapolo iwe wabwino ndi wokhulupirika; unali wokhulupirika pa zinthu zazing'ono, ndidzakhazika iwe pa zinthu zambiri; Iova iwe m'chikondwerero cha mbuye wako**” (Mateyu 25:21).

Yesu akufunanso kuti tidzigwirtsa ntchito ndalamu zathu mwanzeru. “**Musadzikundikire nokha chuma pa dziko lapansi, pamene njenjete ndi dzimbiri ziononga; ndi pamene mbala ziboola ndi kuba: koma mudzikundikire nokha chuma m'Mwamba, pamene njenjete kapena dzimbiri siziononga, ndipo mbala siziboola ndi kuba; pakuti kumene kuli chuma chako, komwe udzakhala mtima wakonso**” (Mateyu 6:19-21).

5. Pamene ophunzira ankalandira chakudya kwa Yesu, ankachigawa kwa anthu a njala. Pamene tikulandira chakudya cha moyo wauzimu kuchokera kwa Yesu, tiyeneranso kugawana ndi iwo otizungulira omwe akusowa “mkate wa moyo.”

Mitundu iwiri ya mkate

Khwimbi la anthu lomwe linali ndi njala linali lokondwera kulandira chakudya. Anafuna kuti Yesu akhale mfumu yao, kuti asakhalenso akuvutika ndi kugwira ntchito kuti apeze chakudya! Koma Yesu anawakumbutsa zomwe zinachitikira makolo awo kale kale. Ana a Israele anali pa ulendo wochokera ku Ejipito kupita ku dziko lomwe Mulungu anawalo-njeza. Gulu la anthu limeneli linamva njala m'chipululu ndipo Mulungu “anawagwetsera” mkate wochokera kumwamba nawadyetsa tsiku ndi tsiku. Ichi chinali chodabwitsa chopambana (Eksodo 16:4-35)! Anthuwo sanadziwe kuti chakudya chatsopanochi chinali chiyani kotero kuti anangochitchula kuti, *mana kutanthauza kuti nchiani ichi?*

Pambuyo pake Mulungu anawaphunzitsa anthu ake chifukwa chimene anachitira izi. Mose anawauza anthuwo nati, **“Ndipo mukumbukire njira yonse imene Yehova Mulungu wanu anakuyendetsani m'chipululu zaka izi makumi anai, kuti akuchepetseni, kukuyesani, kudziwa chokhala mumtima mwanu, ngati mudzasunga malamu-lo ake, kapena iai. Ndipo anakuchepetsani, nakumvetsani njala, nakudyetsani ndi mana, amene simunawa-**



dziwe, angakhale makolo anu sanawadziwe; kuti akudziwitseni kuti munthu sakhala wamoyo ndi mkate wokha, koma munthu akhala wamoyo ndi zonse zakutuluka m'kamwa mwa Yehova” (Deuteronomo 8:2, 3).

Ngakhale kuti Mulungu anawapatsa mana kuchokera kumwamba mu njira yodabwitsa kwa zaka zambiri, mana unali mkate chabe wokhutitsa matupi awo. Anthu amene ankad yawo ankakalambabe ndipo ankafabe. Chimodzimodzinso anthu amene ankadya chakudya chomwe Yesu ankawapatsa chakudyacho chinali cha thupi chabe ndipo ngakhale ankakhuta adakakalambabe pambuyo pake nkufa.

Koma Yesu anali ndi uthenga wopambana! Yesu ankapereka “chakudya” cha mtundu wina chomwe anthu adakadya chidakawapatsa moyo wosatha, osafanso. Ndipo Yesu adakaukitsanso matupi awo patsiku lomaliza pakudza kwake kwachiwiri. Yesu anawauza anthu kuti lye anali chakudya chamtundu wina chomwe anayenera kudya. Anal chakudya *chamoyo* wao wauzimu. Anabwera kuchokera kumwamba ngati m'mene mana anagwera kuchokera kumwamba. Anadza kudzapereka moyo wake kudzikolapansi “Yense wakudya” kapena kulandira ine—moyo wa Khristu, sadzafanso.

‘Tingadye’ bwanji chakudya chamoyochi, chomwe ndi Yesu? ‘Tingamwe’ bwanji mwazi wake? Chofunika ndi kuvo mereza nsembe yomwe Khristu anadzipereka yekha pamtanda kuti tipulumutsidwe. Tikhoza kumulandira Yesu ngati mwana wankhosa wa Mulungu yemwe mwazi wake unga tsuke machimo athu. Tikhoza kulandira mzimu wake womwe umatipatsa moyo pakuwerenga mauwo ndi kuwamvera. Tiyenera kulandira moyo wake *tsiku ndi tsiku* monga m'mene timafunira chakudya kuti matupi athu akhale ndi moyo.

Tikanena za uzimu, mukhoza ‘kudya’ thupi la Yesu ndi ‘kumwa’ mwazi wake tsiku ndi tsiku.

1. Mudziyenda mkuwala kwa mau a Mulungu tsiku ndi tsiku. Ngati mwachimwa, vomerezani tchimo lanu kwa Mulungu, ndipo mwazi wa Yesu udzakusambitsani kuti mupitiri-re kukhala ndi chiyanjano chabwino ndi lye (1 Yohane 1:7, 9).

2. Mudzimupempha Yesu kuti adzikudzazani ndi Mzimu Woyera tsiku ndi tsiku. Mu chilichonse chimene mungachite mudzidalira mphamvu ya mzimu wokhala mwa inu. Tsiku ndi tsiku mudzilandira malangizo ake opeze ka m’Baibuloli. Mau a Mulungu ndiwo moyo kwa ife. Mudzikhala ndi nthawi yapadera inu ndi Mulungu wanu tsiku ndi tsiku. Ndipo mudziyankhula naye mokweza mau. Ndipo mkati mwa tsiku mudziganiza za lye. Mudziyankhula naye m’maganizo mwanu. Mudzaona kuti mwayamba kufanana naye Yesu.

Mulungu ali ndi lonjezano lopambana kwa inu, ngati mutachita zimenezi: “**Pamenepo iwo akuopa Yehova analankhulana wina ndi mnzake; ndipo Yehova anawatcherha khutu namva, ndi buku la chikumbutso linalembedwa pamaso pake, la kwa iwo akuopa Yehova, nakumbukira dzina lake. Ndipo adzakhala angaanga, ati Yehova wa makamu, tsiku ndidzaikalo, ndipo ndidzawaleka monga munthu aleka mwana wake womtumikira**” (Malaki 3:16, 17).

Mau a Mulungu ndi chakudya cha moyo wanu wa uzimu

Zaka zambiri zapitazo Yobu anati, “**Sindinabwerera ku-siya malamulo a pa milomo yake; ndasungitsa mau a pakamwa pake koposa lamulo langalanga**” (Yobu 23:12).

Yeremiya anati, “**Mau anu anapeze ka, ndipo ndinawa-**

dya; mau anu anakhala kwa ine chikondwero ndi chisangalalo cha mtima wanga; pakuti ndatchedwa dzina lanu, Yehova Mulungu wa makamu” (Yeremiya 15:16).

Wolemba Salimo anati, “Mau anu azunadi powalawa ine! Koposa uchi m'kamwa mwanga” (Masalimo 119:103).

Petro analangiza kuti, “Lirani monga makanda alero mkaka woyenera, wopanda chinyengo, kuti mukakule nao kufikira chipulumutso; ngati mwalawa kuti Ambuye ali wokoma mtima” (1 Petro 2:2, 3).

Tiyeni ‘tidye’ mau a Mulungu tsiku ndi tsiku.

PHUNZIRO 12. YESU AYENDA PAMADZI



Yohane 6:16-21

¹⁶Koma pofika madzulo, ophunzira ake anatsikira kunyanja; ¹⁷ndipo pamene adalowa m'ngalawa, analikuoloka nyanja kunka ku Kapernao. Ndipo kutada

pamenepo, koma Yesu asanadze kwa iwo. ¹⁸Ndipo nyanja inalikuuka chifukwa cha mphepo yaikulu yakuombako. ¹⁹Ndipo pamene adapalasa monga mastadiya makumi awiri ndi asanu kapena makumi atatu, anaona Yesu alikuyenda panyanja, ndi kuyandikira ngalawa; ndipo anachita mantha.

²⁰Koma Iye ananena nao, Ndine; musaope. ²¹Pamenepo analola kumlandira m'ngalawa; ndipo pomwepo ngalawayo inafika kumtunda kumene analikunkako.

Zoti muziganizire

Kodi muli mu namondwe? Kodi moyo wanu ukuoneka kuti uli mumdimba waukulu? Kodi Yesu akuoneka kuti ali kutali ndi inu? Kodi inu ndi onse okuzungulirani mukuvutika no-khanokha ndi namondwego? Mukuyesetsa ndi mphamvu yanu yomwe ndi yopelewera kuti mukafikire kutsidya lina? Ngati izi ziri choncho, mudziwe kuti Yesu *amasamala*. *Amdziwa* ndipo *amaona*. Akukuyenderani komwe muliko kudzakumana ndi mavuto anuwo. Musaope. Mulandiren Yesu mokondwera mkatи mwa mavuto anu. Adzakhazikitsa bata m'namondwe wanu ndikukutsogozani *kupita* kutsidya lina la nyanja komwe kuli bata. **“Inde, ndingakhale ndiyenda m'chigwa cha mthunzi wa imfa, sindidzaopa choipa; pakuti Inu muli ndi ine”** (Masalimo 23:4a).

PHUNZIRO 13. YESU ALANKHULA ZA UFULU

Yohane 8:31-37, 42, 47

31Chifukwa chake Yesu ana-nena kwa Ayuda aja adakhu-lupirira Iye, Ngati mukhala inu m'mau anga, muli ophu-nzira anga ndithu; **32**ndipo mudzazindikira choonadi, ndipo choonadi chidzakuma-sulani.

33Anamyankha iye, Tili mbeu ya Abrahamu, ndipo si-tinakhala akapolo a munthu nthawi iliyonse; munena bwanji, Mudzayesedwa afulu?

34Yesu anayankha iwo, nati, Indetu, indetu, ndinena kwa inu kuti yense wakuchita tchi-mo ali kapolo wa chimolo. **35**Koma kapolo sakhala m'nyu-mba nthawi yonse; mwana ndiye akhala nthawi yonse. **36**Chifukwa chake ngati Mwa-na adzakuyesani inu aufulu, mudzakhala mfulu ndithu. **37**Ndidziwa kuti muli mbeu ya Abrahamu; koma mufuna kundipha Ine, chifukwa mau anga alibe malo mwa inu.

42Yesu anati kwa iwo, Mulungu akadakhala Atate wanu, mukadakonda Ine; pakuti Ine ndinatuluka, ndi kucho-kera kwa Mulungu; pakuti sendifinadza kwa Ine ndekha, koma Iyeyu anandituma Ine.

47Iye wochokera kwa Mulungu amva zonena za Mulungu; inu simumva chifukwa chaku-

ti simuli a kwa Mulungu.

Yohane 7:17

17Ngati munthu aliyense afuna kuchita chifuniro chake, adzazindikira za chiphuzitscho, ngati chichokera kwa Mulungu, kapena ndilankhula zochokera kwa Ine ndekha.

Zoti muchite

Mulembe mau ofunikira mu mizere yosalembedwamo:

1. "Yesu anati, ngati _____ inu m'mau anga, ndiyе kuti ndinudi _____ anga" (8:31).
2. Mudzazindikira _____ chidzakumasulani (8:32).
3. Aliyense wochita tchimo ali _____ wa tchimolo (8:34).
4. Ngati _____ adzakumasulani, mudzakhala mfulu ndithu (8:36).
5. Yesu anati, "Mulungu adakakhala Atate wanu, _____ Ine" (8:42).
6. Iye wochokera kwa _____ amva zonena za Mulungu (8:47).
7. Munthu aliyense wofuna kuchita _____ adzazindikira za _____ ngati chichokera kwa Mulungu (7:17).

PHUNZIRO 14. YESU NDIYE KUUNIKA KWA DZIKO LAPANSI



Yohane 8:12

¹²Pamenepo Yesu analankhulanso nao, nanena, Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi; iye wonditsata Ine sadzayenda mumdimma, koma adzakhala nako kuunika kwa moyo.

Yohane 9:1-9, 13-25, 33-38

¹Ndipo popita, anaona munthu ali wosaona chibadwire.
²Ndipo ophunzira ake anamfunsa Iye, nanena, Rabi, anachimwa ndani, ameneyo, kapena atate wake ndi amake, kuti anabadwa wosaona?

³Yesu anayankha, Sanachimwe ameneyo, kapena atate wake ndi amake; koma kuti ntchito za Mulungu zikao-netsedwe mwa iye. ⁴Tiyenera kugwira ntchito za Iye wondituma Ine, pokhala pali msana; ukudza usiku pamene palibe munthu angakhoze kugwira ntchito. ⁵Pakukhala Ine m'dziko lapansi, ndili kuunika kwa dziko lapansi. ⁶Pamene ananena izi, analavula pansi, nakanda thope ndi malovuwo, napaka thopelo m'maso, ⁷nati kwa iye, Muka, kasambe m'thamanda la Siloamu (ndilo losandulika, Wotumidwa). Pamenepo anachoka, nasamba, nabwera ali-kuona.

⁸Chifukwa chake anzake ndi iwo adamuona kale, kuti anali wopemphapempha, ananena, Kodi si uyu uja wokhala ndi kupemphapempha? ⁹Ena ananena, kuti, Ndiyeyu; ena ananena, Iai, koma afanana naye. Iyeyu anati, Ndine amene.

¹³Anapita naye amene anali wosaona kale kwa Afarisi.

¹⁴Koma tsikulo ndi la Sabata limene Yesu anakanda thope, namtsegulira iye maso ake.

¹⁵Pamenepo ndipo Afarisi anamfunsanso, umo anape-nyera. Ndipo anati kwa iwo, Anapaka thope m'maso mwanga, ndinasamba, ndipo ndi-penya. ¹⁶Ena pamenepo mwa Afarisi ananena, Munthu uyu sachokera kwa Mulungu, chifukwa sasunga Sabata. Koma ena ananena, Munthu ali wo-chimwa akhoza bwanji kuchi-ta zizindikiro zotere? Ndipo panali kutsutsana mwa iwo.

¹⁷Pamenepo ananenanso kwa wosaonayo, Iwe unenanji za Iye, popeza anakutsegulira maso ako? Koma iye anati, Ali Mneneri. ¹⁸Chifukwa chake Ayuda sanakhulupirire za iye, kuti anali wosaona, napenya, kufikira kumene adaitana atate wake ndi amake a iye wopenya; ¹⁹nawafunsa iwo, nanena, Kodi uyu ndi mwana wanu, amene inu munena kuti anabadwa wosaona? ²⁰Ndipo apenya bwanji tsopano? Atate wake ndi amake anayankha

nati, Tidziwa kuti uyu ndi mwana wathu, ndi kuti ana-badwa wosaona; ²¹koma siti-dziwa uno apenyera tsopano; kapena sitimdziwa mene ana-mtsegulira pamaso pake; mu-mfunse iye; ali wamsinkhu; adzalankhula mwini za iye ye-kha. ²²Izi ananena atate wake ndi amake, chifukwa anaopa Ayuda; pakuti Ayuda adap-a-nanga kale, kuti ngati munthu aliyense adzamvomereza Iye kuti ndiye Khristu, akhale woletsedwa m'sunagogue.

²³Chifukwa cha ichi atate wa-ke ndi amake anati, Ali wa-msinkhu; mumfunse iye. ²⁴Pamenepo anamuitana ka-chiwiri munthuyo amene anali wosaona, nati kwa iye, Le-mekeza Mulungu; tidziwa ku-ti munthuyo ali wochimwa.

²⁵Pamenepo iyeyu anaya-nkha, Ngati ali wochimwa, si-nnidziwa; chinthu chimodzi ndichidziwa, pokhala ndinali wosaona, tsopano ndipenya. ³³Ngati uyu sanachokera kwa Mulungu, sakadakhoza ku-chita kanthu. ³⁴Anayankha nati kwa iye, Wabadwa iwe konse m'zoipa, ndipo iwe uti-

phunzitse ife kodi? Ndipo anamtaya kunja.³⁵ Yesu anamva kuti adamtaya kunja; ndipo pakumpeza iye, anati, Kodi ukhulupirira Mwana wa Munthu?³⁶ Iyeyu anayankha nati, Ndipo ndani Iye,

Ambuye, kuti ndimkhulupirire Iye?³⁷ Yesu anati kwa iye, Wamuona Iye, ndiponso wakulankhula ndi iwe ndi Iyeyo.³⁸ Koma iye anati, Ndikhulupirira, Ambuye; ndipo anamgwadira Iye.

Adanena izi ndani?

1. Ndani adanena mau akuti, "Ukudza usiku pamene palibe munthu angakhoze kugwira ntchito?" _____ (vesi 4).

2. Ndani adanena mau akuti, "Kodi si uyu uja wokhala ndi kumangopemphapempha?" _____ (8).

3. Ndani adanena mau akuti, "Munthu uyu sachokera kwa Mulungu?" _____ (16).

[Afarisi linali gulu la Ayuda chipembedzo cha Chiyuda. Ankatsatira kwambiri ndi kuloweza malamulo a Mose ndi miyambo ya makolo.]

4. Ndani adanena mau akuti, "Ali wamsinkhu mumfunse iye," chifukwa ankaopa akulu a Ayuda? _____ (21-23).

[Inali nkhani yovuta kwambiri munthu ukatulutsidwa mu sunagogue. Wotulutsidwayo ankachitiridwa zoipa ngati wakhate. Palibe ankaloledwa kudya naye pamodzi kapena kuchita naye malonda.]

5. Ndani ananena mau akuti, "Ngati uyu sanachokera kwa Mulungu, sakadakhoza kuchita kanthu?" _____ (33).

6. Ndani adanena mau akuti, "Kodi ukhulupirira mwana wa Munthu?" _____ (35).
7. Ndani adanena mau akuti, "Ambuye ndimkukhulupirira lye"? _____ (38).

Yesu abweretsa kuunika

Yesu atatsekula maso a munthu wakhungu, anabweretsa kuunika m'moyo mwake. Koma Yesu anafuna kuonetsa kuti anabwera kudzatsekula maso a uzimu a anthu *onse* okhala mumdimba.

Nthawi imeneyo nkuti Mulungu atalonjeza kale kudzera mwa aneneri ake kuti wina adzabwera yemwe adzabwerte-tse kuwala. Mulungu anaftokoza za Yesu motere, "**Ine Yehova ndakuitana Iwe m'chilungamo, ndipo ndidzawira dzanja lako ndi kusunga Iwe, ndi kupatsa Iwe ukhale pangano la anthu, ndi kuunika kwa amitundu; kuti utsegule maso akhungu, utulutse am'nsinga m'nde-nde, ndi iwo amene akhala mumdimba, atuluke m'nyumba ya kaidi**" (Yesaya 42:6, 7). Yesaya anaiwona nthawi imene Yesu anakhalamo nati, "**Anthu amene anayenda mumdimba, aona kuwala kwakukulu; iwo amene anakha-la m'dziko la mthunzi wa imfa, kuwala kwatulukira kwa iwo**" (Yesaya 9:2).

Pamene Yesu ankanena kuti iye ndi kuunika kwa dziko lapansi, Ayuda anadziwa kuti Yesu ankanena kuti iye ndiye Mulungu chifukwa Mulungu ndiye kuunika "**Yehova ndiye kuunika kwanga ndi chipulumutso changa**" (Masalimo 27:1a). "**Pokhala ine mumdimba Yehova adzakhala kuunika kwanga**" (Mika 7:8b). Poyamika Mulungu Davide anati, "**Pakuti Inu ndinu nyali yanga, Yehova; ndipo Yehova adzaunika mumdimba mwanga**" (2 Samuele 22:29).

Tikamodziwa Yesu, ndiye kuti tadziwana ndi Mulungu. Yesu anati, “**Mukadazindikira lne mukadadziwa Atate wanguanso**” (Yohane 14:7a). “**Pakuti Mulungu amene anati, Kuunika kudzawala kutuluka mumdima, ndiye amene anawala m'mitima yathu kutipatsa chiwalitsiro cha chidziwitso cha ulemerero wa Mulungu pankhope pa Yesu Khristu**” (2 Akorinto 4:6). Kodi mwakulandira kuunika kumeneku?

Kuyenda mkuunika

Onse otsatira Yesu sayenda mumdima, koma mkuunika. “**Pakuti kale munali mdima, koma tsopano muli kuunika mwa Ambuye; yendani monga ana a kuunika**” (Aefeso 5:8).

“**Njira ya oipa ikunga mdima; sadziwa chimene chiphunthwitsa**” (Miyambo 4:19). “**Koma mayendedwe a olungama akunga kuunika kwa mbandakucha, kunkabe kuwala kufikira usana woti mbée**” (Miyambo 4:18).

Mau a Mulungu ndiwo kuunika. “**Mau anu ndiwo nyali ya ku mapazi anga, ndi kuunika kwa panjira panga**” (Masalimo 119:105). “**Potsegulira mau anu paunikira; kuzindikiritsa opusa**” (Masalimo 119:130). Pamene tikuwerenga mau a Mulungu tsiku ndi tsiku, *tidzitchera khutu* ndi *kumvera zomwe akunena*. Ili ndilo tanthauzo la “kuyenda mkuunika,” *kuchita zimene Mulungu akunena* ndiko kuyenda mkuunika. Kodi mukukumbukira lamulo la Yesu lonena kuti tidzikondana wina ndi mzake? Ichi ndi chifukwa chake mau a Mulungu amanena kuti, “**Koma iye wakumuda mbale wake ali mumdima, nayenda mumdima, ndipo sadziwa kumene amukako, pakuti mdima wamdetsa maso ake**” (1 Yohane 2:11).

Njira yachidule yoti munthu akhale wakhungu ndiyo ku-

yenda mumdima nthawi zonse. Abulu amene amagwiritsidwa ntchito ku mgodi wa malasha, amayenera kutulutsidwa kunja kamodzi pa Sabata. Atangokhaliratu ku mgodi osatulutsidwa kunja akhoza kuchita khungu. Ndi chimodzimodzinso ndi ife, *tiyenera* kuyenda mkuunika, kupanda kutero maso athu auzimu angachite khungu.

Ndife kuunika kwa dziko lapansi

“Chitani zonse kopanda madandaulo ndi makani, kuti mukakhale osalakwa ndi oona, ana a Mulungu opanda chilema pakati pa mbadwo wokhotakhota ndi wopotoka, mwa iwo amene muonekera monga mauniko m'dziko lapansi” (Afilipi 2:14, 15). Mulungu watisankha ife kuti, “**mukalalikire zoposazo za lye amene anakuitanani mutuluke mumdima, mulowe kuunika kwake kodabwitsa**” (1 Petro 2:9b). Kodi moyo *wanu* umawalira ena omwe akuzungulirani? Ngati sichoncho, mtumwi Paulo akunena kuti, **“chake tivule ntchito za mdima, ndipo tivale zida za kuunika”** (Aroma 13:12b).

Tiyenera kukhala okonzekera kubweranso kwa Ambuye wathu. Tikhoza kukhala okonzeka pokhapokha ngati titadzuka komanso kuyenda mkuunika. **“Pakuti inu nonse muli ana a kuunika, ndi ana a usana; sitili a usiku, kapena a mdima; chifukwa chake tsono tisagone monga otsalawo, komatu tidikire, ndipo tisaledzere”** (1 Atesalonika 5:5, 6).

Ponena za kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano, Yesu ananena za Yerusalemu watsopano kuti, **“Ndipo pamzinda sipafunika dzuwa, kapena mwezi wakuualira; pakuti ulemerero wa Mulungu uunikira umenewu, ndipo nyali yake ndiye Mwanawankhosa”**

(Chivumbulutso 21:23). Kodi sizonyaditsa kuti Yesu adzakhalala kuunika kwathu kwamuyaya!

Kugwira ntchito kukadali kuwala

Tiyenera kugwira ntchito kukadali kuwala mdziko la mdimali mpaka Yesu atabwera. Tsiku lina dzikoli lidzatha (Mateyu 5:18). Iwo amene sanabwera ku kuwala adzatsikira kumdima wakunja komwe adzakhale kwamuyaya. (Mateyu 22:13). Tiyeni tigwire ntchito “**kukawatsegulira maso ao, kuti atembenuke kuchokera kumdima, kulinga kukuunika, ndi kuchokera ulamuliro wa Satana kulinga kwa Mulungu, kuti alandire iwo chikhululukiro cha machimo**” (Machitidwe a Atumwi 26:18a).

Ayuda nthawi ina anamfunsa Yesu kuti, “**Tichite chiyani, kuti tichite ntchito za Mulungu?**” (Yohane 6:28). Yesu anayankha nati, “**Ntchito ya Mulungu ndi iyi, kuti mukhulupirire lye amene lyeyo anamtuma**” (Yohane 6:29). Yesu adaphunzitsa momveka bwino kuti, “**Pakuti ngati simukhulupirira kuti Ine ndine, mudzafa m'machimo anu**” (Yohane 8:24b).

Choyamba pakhale chitsimikizo kuti tili mkuwala kuti tilandire moyo wosatha. Tikatero tigwire ntchito pamodzi *ndi* Yesu *yobweretsa* ena kuwala. “**Gwirani ntchito si chifukwa cha chakudya chimene chitsalira kumoyo wosatha, chimene Mwana wa Munthu adzakupatsani inu**” (Yohane 6:27a).

Kodi mukukumbukira nkhani yamunthu wa khungu yomwe tayiphunzira. Anauza ena *molimba mtima* zimene Yesu anamuchitira. Ngakhale anthu omwe anali akhungu mu uzimu anamuponya kunja, Yesu anamusamalira nabwera kwa *iyekudzadziulula* yekha. Akhozanso kuchita izi kwa inunso!

PHUNZIRO 15. YESU NDIYE M'BUSA WABWINO



Yohane 10:1-16, 27-33

1Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Iye wosalowa m'khola la nkhosa pakhomo, koma akwerera kwina, iyeyu ndiye wakuba ndi wolanda. **2**Koma iye wakulowera pakhomo, ndiye mbusa wa nkhosa. **3**Iyeyu, wa-pakhomo amtsegulira ndi nkhosa zimva mau ake; ndipo aitana nkhosa za iye yekha maina ao, nazitsogolera kujna. **4**Pamene adatulutsa zonse nkhosa zimtsata iye; chifukwa zidziwa mau ake. **5**Koma mlendo sizidzamtsata, koma zdzamthawa; chifukwa sizidziwa mau a alendo. **6**Fanizo ili

Yesu ananena kwa iwo; koma sanazindikira zimene Yesu analikulankhula nao. **7**Chifukwa chake Yesu ananenanso nao, Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Ine ndine khomo la nkhosa. **8**Onse amene anadza m'tsogolo mwa Ine ali akuba, ndi olanda: koma nkhosa sizinamva iwo. **9**Ine ndine khomo; ngati wina a lava ndi Ine, adzapulumutsidwa, nadzalowa, nadzatuluka, nadzapeza busa. **10**Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga. Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wochuluka. **11**Ine ndine Mbusa Wabwino; mbusa wabwino ataya moyo wake chifukwa cha nkhosa. **12**Wolipidwa amene sakhala mbusa, amene nkhosa sizili zake za yekha, aona mmbulu ulinkudza, nasiya nkhosazo, nathawa; ndipo mmbulu uzikwatala, nuzibalalitsa; **13**chifukwa ali wolipidwa, ndipo sasamala nkhosa. **14**Ine ndiye Mbusa Wabwino; ndipo ndizindikira zanga, ndi zanga zindizindiki-

ra Ine,¹⁵ monga Atate anddziwa Ine, ndi Ine ndimdziwa Atate; ndipo nditaya moyo wanga chifukwa cha nkhosa.

¹⁶Ndipo nkhosa zina ndili nazo, zimene sizili za khola ili; izinso ndiyenera kuzitenga, ndipo zidzamva mau anga; ndipo zidzakhala gulu limodzi, mbusa mmodzi.

²⁷Nkhosa zanga zimva mau anga, ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine.

²⁸Ndipo Ine ndizipatsa moyo wosatha; ndipo sизidzaonongeka kunthawi yonse, ndipo palibe munthu adzazikwatula m'dzanja langa. ²⁹Atate wa-

nga, amene anandipatsa izo, ali wamkulu ndi onse; ndipo palibe wina ngathe kuzikwatala m'dzanja la Atate. ³⁰Ine ndi Atate ndife amodzi. ³¹Ayuda anatolanso miyala kuti amponye Iye. ³²Yesu anayankha iwo, Ndakuonetsani inu ntchito zabwino zambiri za kwa Atate; chifukwa cha ntchito yiti ya izo mundiponya miyala? ³³Ayuda anamyanckha Iye, Chifukwa cha ntchito yabwino sitikuponyani miyala, koma chifukwa cha mwano; ndi kuti Inu, muli munthu, mudziyesera nokha Mulungu.

Zomwe taphunzira mu phunziroli

1. Yesu ndi khomo lokhala lolowera ku chipulumutso. Tikoza kukhala nkhosa zake pakumva mau ake ndi kumutsatira. Amakuitanani potchula dzina lanu, amakutsogolerani, amakupatsani msipu wabwino, amapereka moyo wake chifukwa cha inu. **“Tonse tasochera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa lye mphulupulu ya ife tonse”** (Yesaya 53:6). Kodi mwasankha kusiya njira zanu ndikumtsatira njira yake?

2. Yesu ndiye mbusa weniweni. **“Pakuti lye ndiye**

Mulungu wathu, ndipo ife ndife anthu a pabusa pake” (Masalimo 95:7a). “**Dziwani kuti Yehova ndiye Mulungu; lyeyu anatilenga, ndipo ife ndife ake; ndife anthu ake ndi nkhoa zapabusa pake”** (Masalimo 100:3).

3. *Ngati tili nkhoa zake, amatidziwa ndipo ifenso timamudziwa.* “**Koma inu, Yehova, mundidziwa ine; mundiona ine, moyesa mtima wanga ngati utani nanu**” (Yeremiya 12:3a). *Kodi mukumudziwa Yesu ngati mbusa wanu?* Ngati mukumudziwadi, mudzamutsatira lye yekha basi. *Kodi mbusayo amakudziwani?* “**Mbusa wamkulu akadzatulukira,**” ambiri adzamuza kuti, “**Ambuye, Ambuye, kodi sitinanenera mau m'dzina lanu, ndi m'dzina lanunso kutulutsa ziwanda, ndi kuchita m'dzina lanunso zamphamvu zambiri?**” (Mateyu 7:22). Yesu akunena kuti, “**Ndipo pamene po ndidzafukulira iwo, Sindinakudziwani inu nthawi zonse; chokani kwa Ine, inu akuchita kusaweruzika**” (Mateyu 7:23). Sitingakhale ake a mbusayo nkumachitanso zofuna zathu nthawi yomweyo, popanda chiyero palibe munthu amene adzaone Ambuye (Ahebri 12:14).

4. *Pamene tili ake a Yesu, ndife otetezedwa kwamuyaya.* Palibe angatikwatule m'dzanja lake. Lonjezano limeneli ndi loperekedwa kwa okhao amene akutsata mbusa wamkulu wa nkhoa, Ambuye Yesu Khristu.

5. *Iye wotsatira Yesu adzawachokera anthu achilendo.* Satana ali ngati wakuba yemwe akufa, akuba, kupha ndi kuononga.

6. *Yesu ankanena kuti lye anali Mulungu.* Koma Yesu atanena kuti anali mbusa wabwino komanso kuti lye ndi Atate anali m'modzi, Ayuda anadziwa kuti lye ankadzifanizira ndi Mulungu. Akadakhala otsatira a Mulungu, adakamuzindikira Yesu kuti anali mbusa wao. Yesaya analosera kuti,

“Taonani, Ambuye Yehova adzadza.... lye adzadyetsa zoweta chake ngati mbusa, nadzasonkhanitsa anaankhosa pachepta pake, nadzawatengera pa chifuwa chake, ndipo adzatsogolera bwinobwino zimene ziayamwitsa” (Yesaya 40:10, 11).

Salmo la Mbusa

Masalimo 23

1Yehova ndiye mbusa wanga; sindidzasowa. 2Andigonetsa kubusa lamsipu, anditsogolera kumadzi odikha. 3Atsitsimutsa moyo wanga; anditsogolera m'mabande a chilungamo, chifukwa cha dzina lake. 4Inde, ndingakhale ndiyenda m'chigwa cha mthunzi wa imfa, sindidzaopa choipa; pakuti Inu muli ndi ine; chibonga chanu ndi ndodo yanu, izi zindisangalatsa ine. 5Mundiyalikira gome pamaso panga m'kuona kwa adani anga; mwandidzoza mutu wanga mafuta; chikho changa chisefuka. 6Inde ukoma ndi chifundo zidzanditsata masiku onse a moyo wanga, ndipo ndidzakhala m'nyumba ya Yehova masiku onse.



PHUNZIRO 16. YESU NDI KUUKA NDI MOYO

Yohane 11:1-7, 17-46

¹Koma panali munthu wdwala, Lazaro wa ku Betanya, wa m'mudzi wa Maria ndi mbale wake Marita. ²Koma ndiye Maria uja anadzoza Ambuye ndi mafuta onunkhira bwino, napukuta mapazi ake ndi tsitsi lake, amene mlongo wake Lazaro anadwala. ³Pamenepo alongo ake anatumiza kwa Iye, nanena, Ambuye, onani, amene mumkonda adwala. ⁴Koma Yesu pamene anamva, anati, Kudwala kumene sikuli kwa imfa, koma chifukwa cha ulemerero wa Mulungu, kuti Mwana wa Mulungu alemekezedwe nako.

⁵Koma Yesu anakonda Marita, ndi mbale wake, ndi Lazaro. ⁶Chifukwa chake pamene anamva kuti anadwala, anakhala pamenepo pa malo pomwepo masiku awiri. ⁷Ndipo pambuyo pake ananena kwa ophunzira ake, Tiyeni tipitenso ku Yudeya.

¹⁷Ndipo pamene Yesu andaiza, anapeza kuti pamenepo

atakhala m'manda masiku anai. ¹⁸Koma Betaniya anali pafupi pa Yerusalem, nthawi yake yonga ya mastadiya khu-mi ndi asanu; ¹⁹koma ambiri a mwa Ayuda adadza kwa Marita ndi Maria, kudzawatonthoza mtima pa mlongo wao. ²⁰Pamenepo Marita, pakumva kuti Yesu alinkudza, anamuka kukakomana ndi Iye; koma Maria anakhalabe m'nyumba. ²¹Ndipo Marita anati kwa Yesu, Ambuye, mu-kadakhala kuno mlongo wanga sakadafa. ²²Koma ngakhale tsopano ndidziwa kuti zinthu zilizonse mukapempha Mulungu, adzakupatsani Mulungu. ²³Yesu ananena naye, Mlongo wako adzauka. ²⁴Marita ananena ndi Iye, Ndidiwa kuti adzauka m'kuuka tsiku lomaliza. ²⁵Yesu anati kwa iye, Ine ndine kuuka ndi moyo: wokhulupirira Ine, angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo; ²⁶ndipo yense wakukhala ndi moyo, nakhu-

lupirira Ine, sadzamwalira nthawi yonse. Kodi ukhulu-pirira ichi? ²⁷Ananena ndi Iye, Inde Ambuye; ndakhu-lupirira ine kuti Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulu-nku, wakudza m'dziko lapa-nси.

28Ndipo m'mene anati ichi anachoka naitana Maria mbale wake m'tseri, ndi kuti, Wafika Mphunzitsi, akuitana iwe. ²⁹Koma iyeyo, pakumva, ananyamuka msanga, nadza kwa Iye. ³⁰(Koma Yesu sana-fike kumudzi, koma anali pamalo pomwe Marita adako-mana ndi Iye.) ³¹Pamenepo Ayuda okhala naye m'nyu-mba, ndi kumtonthoza iye, pakuona Maria ananyamuka msanga, natuluka, namtsata iye, ndi kuyesa kuti amuka kumanda kukalira komweko. ³²Pomwepo Maria, pofika pamene panali Yesu, m'mene anamuona Iye, anagwa pa mapazi ake, nanena ndi Iye, Ambuye, mukadakhala kuno Inu, mlongo wanga saka-damwalira.

33Pamenepo Yesu, paku-muona iye alikulira, ndi

Ayuda akumperekeza iye ali-kulira, anadzuma mumzimu, navutika mwini, ³⁴nati, Mwa-muika iye kuti? Ananena ndi Iye, Ambuye, tiyeni mukaone.

35Yesu analira. ³⁶Chifukwa chake Ayuda ananena, Taona-ni, anamkondadi! ³⁷Koma ena mwa iwo anati, Kodi uyu wo-tsegulira maso wosaona uja, sanakhoza kodi kuchita kuti sakadafa ameneyunso? ³⁸Pa-menepo Yesu, ndi kudzuma-nso mwa Iye yekha anadza kumanda. Koma panali pha-nga, ndipo mwala unaikidwa pamenepo. ³⁹Yesu ananena, Chotsani mwala. Marita, mlo-ngo wake wa womwalirayo, ananena ndi Iye, Ambuye, adayamba kununkha: pakuti wagona masiku anai. ⁴⁰Yesu ananena naye, Kodi sindinati kwa iwe, kuti, ngati ukhu-lupirira, udzaona ulemerero wa Mulungu? ⁴¹Pomwepo anachotsa mwala. Koma Yesu anakweza maso ake kupenya kumwamba nati, Atate, ndi-yamika Inu kuti munamva Ine. ⁴²Koma ndadziwa Ine kuti mumandimva Ine nthawi zonse; koma chifukwa cha



khamu la anthu aliquimirira pozungulira ndinanena ichi, kuti akhulupirire kuti Inu munandituma Ine. ⁴³Ndipo

m'mene adanena izi, anafuula ndi mau akulu, Lazaro, tulu-ka. ⁴⁴Ndipo womwalirayo anatuluka womangidwa miye-ndo ndi manja ndi nsalu za kumanda; ndi nkhope yake inazingidwa ndi mlezo. Yesu ananena nao, Mmasuleni iye, ndipo mlekeni amuke. ⁴⁵Chifukwa chake ambiri a mwa Ayuda amene anadza kwa Maria, m'mene anaona chimene anachita, anakhu-lupirira Iye. ⁴⁶Koma ena a mwa iwo anamuka kwa Afarisi, nawauza zimene Yesu adazichita.

Zoti muziganizire

Kodi sizabwino kudziwa kuti Yesu anawakonda abwenzi ake kwambiri? Inunso ndinu bwenzi lake, ngati mutamachi-ta zomwe amanena (Yohane 15:14). Mu nkhani iyi, abwenzi ake a Yesu anali ndi chisoni. M'bale Lazaro anamwalira. Po-yamba zinaoneka ngati kuti Yesu sizinamukhudze. Kodi nthawi zina mumaona ngati Mulungu sizikumukhudza pa mavuto amene mukukumana nao? Komatu Mulungu sago-na. Nthawi zonse amakhala ndi dongosolo. Tidzimukhulu-pilira nthawi zonse akhoza kutichitira zinthu zomwe

pambuyo pake zibweretse ulemerero ku dzina la Mulungu.

Mulungu ali nalo dongosolo pa moyo wanunso. Akufuna kukukonzani kuti mukhale ngati mwana wake Yesu Khristu. **“Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwachitira ubwino, ndiwo amene aitanidwa monga mwa kutsimikiza kwa mtima wake. Chifukwa kuti iwo amene lye anawadziwiratu, iwowa anawalamuliratu afanizidwe ndi chifaniziro cha Mwana wake, kuti lye akakhale mwana woyamba wa abale ambiri”** (Aroma 8:28, 29). Ichi ndi chifukwa chake tiyenera kukumana ndi nyengo zovuta. **“Kuti mayesedwe a chikhulupiriro chanu, ndiwo a mtengo wake woposa wa golide amene angotayika, ngakhale ayesedwa ndi moto, akapezedwe ochitira chiyamiko ndi ulemerero ndi ulemu pa vumbulutso la Yesu Khristu”** (1 Petro 1:7).

Yesu ankafuna kumuphunzitsa Maria ndi Marita komanso ife kuti kukhulupirira lye kumatanthauza kuti sitidzafa. Okhulupirira Yesu akafa, ndiye kuti kwaiwo kuli, **“ndipo tikondwera makamaka kusakhala m’thupi, ndi kukhala kwathu kwa Ambuye”** (2 Akorinto 5:8).

Yesu anatsimikiziranso kuti akhoza kupereka moyo kwa matupi akufa pongoitana dzina la munthu wakufayo. Lazaro anamva mau a Yesu pomwe anamuitana, ndipo anakhala ndi moyo. Yesu akadzabweranso ku dziko lapansi, pamene **“akufa adzamva mau a Mulungu; ndipo iwo akumva adzakhala ndi moyo”** (Yohane 5:25b).

Ngakhale tsopano lino Yesu akugogoda pakhomo la mitima, **“Wina akamva mau anga nakatsegula pakhomo, ndidzalowa kwa iye...”** (Chivumbulutso 3:20b).

Iwo akumva mau ake ndi kutsekula chitseko adzakhala

olengedwanso mwatsopano. “Ndipo inu, anakupatsani moyo, pokhala munali akufa ndi zolakwa, ndi zochimwa zanu” (Aefeso 2:1). “Chotero inunso mudziwerengere inu nokha ofafa ku uchimo, koma amoyo kwa Mulungu mwa Khristu Yesu. Chifukwa chake musamalola uchimo uchite ufumu m’thupi lanu la imfa kumvera zofuna zake: ndipo musapereke ziwalo zanu kuuchimo, zikhale zida za chosalungama; koma mudzipereke inu nokha kwa Mulungu, monga amoyo atatuluka mwa akufa, ndi ziwalo zanu kwa Mulungu zikhale zida za chilungamo” (Aroma 6:11-13).

Kumvera kumafunikira kuti chodabwitsachi chichitike

Kodi mwataya mtima ndi zovuta zina ndipo pakusoweka chodabwitsa? Yesu akhoza kulolera kuti mupezane ndi nthawi yovuta m’moyo mwanu, “chifukwa cha ulemerero wa Mulungu.” Koma musaiwale kuti amakukondani momwe anakondwera Maria ndi Marita. Mwina wakukonzerani chodabwitsa chomwe simunayembekezere. Koma taonani kufunikira kwa kumvera komwe kunachititsa kuti chodabwitsa pa moyo watsopano chichitike. Yesu anati, “Chotsani mwala.” Ngakhale anaona ngati chinthu chooneka chopusa, komabe anamvera. Lazaro atatuluka m’manda, Yesu anati, “M’masuleni iye, ndipo mumleke amuke.”

Pofuna kuona ulemerero ndi mphamvu ya Mulungu, ifenso tiyenera kukhala omvera ngakhale pa zazing’ono zimene

Mzimu Woyerangatiuze. Ngati kuli kofunika kumupe-mpha munthu kuti atikhulu-lukire titalakwa ngakhale pang'ono pokha, tiyenera kutero. Mwina ungakhale mwala umene ukufunika kuti mukachotse kuti Yesu achite zodabwitsa m'moyo wa munthu wina. Ndipo Yesu akachita zodabwitsa tiyeni tithandize mwachikondi kumasula ena ku zinthu zonse zingawalepheretse iwo kulandira ufulu uwu. Kodi sizodabwitsa kuti Yesu anavomereza abwenzi ake kuti athandizepo kuti chodabwitsachi chichitikedi?



PHUNZIRO 17. AKULU A ULAMULIRO APANGANA ZA KUPHA YESU

Yohane 11:47-53

47Pamenepo ansembe aaku-
lu ndi Afarisi anasonkhanitsa
akulu, nanena, Titani ife? Chifukwa munthu uyu achita
zizindikiro zambiri. **48**Ngati
timleka Iye kotero, onse adza-
khulupirira Iye; ndipo adza-

dza Aroma nadzachotsa malo
athu ndi mtundu wathu.
49Koma wina mmodzi wa
mwa iwo, Kayafa, wokhala
mkulu wa ansembe chaka
chomwecho anati kwa iwo, Si-
mudziwa kanthu konse inu,

⁵⁰kapena simuganiza kuti nkokoma kwa inu kuti munthu mmodzi afere anthu, ndi kuti mtundu wonse usaonongeke. ⁵¹Koma ichi sanane-na kwa iye yekha; koma pokhala mkulu wa ansembe chaka chomwecho ananenera

kuti Yesu akadzafera mtu-nduwo; ⁵²ndipo si chifukwa cha mtunduwo wokha ai, ko-ma kuti akasonkhanitse pa-modzi ana a Mulungu akuba-lalikawo. ⁵³Chifukwa chake, kuyambira tsiku lomwelo anapangana kuti amuphe Iye.

Kukanidwa kwa mfumu

Gulu lolamulira la chiyuda linaona zodabwitsa za Yesu. Anamumva akuphunzitsa kuti lye ndi Atate anali m'modzi komanso kuti lye analipo asanabwere Abrahamu ku dziko lapansi (Yohane 8:58). Ngakhale izi zinali choncho sanakhulupire kuti Yesu anali mfumu yolonjezedwa ya Israele.

Nkhaniyi ikuonetsa ngati kuti atsogoleri achiyuda sanali okonzekera kusiya maudindo ao. Analu ngati antchito oyipa omwe Yesu anawafotokozeru mu fanizo lake. Antchitowo anati, "**Ife sitifuna munthuyo akhale mfumu yathu**" (Luka 19:14b). Chifukwa cha ichi atsogoleri achiyuda anaganiza zomupha munthuyu, Yesu kuti mtundu wao ukhale otetezedwa. Komabe iwo sadakatha kuchita kanthu Yesu adakapanda *kupereka moyo wake*.

Chikonzero cha Mulungu dziko lisanakhazikike chinali choti Yesu adzapulumutse dziko lonse lapansi osati mtundu wa Israele wokha! "**Koma kunakomera Yehova kumtundudza; anammvetsa zowawa; moyo wake ukapereka nsembe yopalamlula, lye adzaona mbeu**

yake,... ndipo chomkondweretsa Yehova chidzakula m'manja mwake" (Yesaya 53:10).

PHUNZIRO 18. NKHANI YA MPHATSO YA MTENGO WAPATALI



Yohane 12:1-8

1Pomwepo anatsala masiku asanu ndi limodzi asanafike Paska, Yesu anadza ku Beta- niya kumene kunali Lazaro, amene Yesu adamuukitsa kwa akufa. **2**Ndipo anamkonzera Iye chakudya komweko; ndipo Marita anatumikira; koma Lazaro anali mmodzi wa iwo akuseama pachakudya pamodzi ndi Iye. **3**Pamenepo Maria m'mene adatenga muyeso umodzi wa mafuta onunkhira

bwino a narido weniweni a mtengo wake wapatali, ana- dzoza mapazi a Yesu, napuku- ta mapazi ake ndi tsitsi lake; ndipo nyumba inadzazidwa ndi mnunkho wake wa ma- futawo. **4**Koma Yudas Iska- riote, mmodzi wa ophunzira ake, amene adzampereka Iye, ananena, **5**Nanga mafuta onu- khira awa sanagulitsidwa chifukwa ninji ndi marupiya atheka mazana atatu, ndi ku- patsidwa kwa osauka? **6**Koma ananena ichi si chifukwa ana- likusamalira osauka, koma chifukwa anali mbala, ndipo pokhala nalo thumba, amaba zoikidwamo. **7**Pamenepo Yesu anati, Mleke iye, pakuti ana- chisungira ichi tsiku la kuikitwa kwanga. **8**Pakuti osauka muli nao pamodzi ndi Ine nthawi zonse; koma simuli ndi Inu nthawi zonse.

Yesu ndi woyenera ulemu wonse

Yesu atamuukitsa Lazaro Akulu akulu achiyuda, anagwirizana kuti amuphe Yesu. Koma abwenzi ake a Yesu anakondwera ndi kuyamika koteru kuti anakonza chakudya chapadera pomulemekeza Yesu. Maria anamudziwa Yesu kuti anali wotani. Chikondi chake chinamupangitsa kukagula mafuta onunkhira a mtengo wapatali—mtengo wake unali wofanana ndi malipiro a chaka chonse a munthu wolementwa ntchito. Maria anamvetsetsa mau a Yesu onena kuti adzayenera kupachikidwa posachedwa (Mateyu 26:2).

“Muyenera inu, Ambuye wathu, ndi Mulungu wathu, kulandira ulemerero ndi ulemu ndi mphamvu; chifukwa mudalenga zonse, ndipo mwa chifuniro chanu zinakhalia, nizinalengedwa” (Chivumbulutso 4:11).

Yohane akutipatsa chithunzi cha m'mene zidzakhalire kumwamba, pomwe owomboledwa a mitundu yonse, mafuko ndi zinenero zosiyansiyana adzakhale pamodzi ndi zikwizikwi za angelo kulemekeza Yesu, **“Ayenera Mwanawankhosa, wophedwayo, kulandira chilimbiko, ndi chuma, ndi nzeru, ndi mphamvu, ndi ulemu, ndi ulemerero, ndi chiyamiko”** (Chivumbulutso 5:12b). Yesu ndi woyenera matamando ndi kumpembedza momwe tingathere!

Mphatso zomwe tingamupatse Yesu

Tingamupatse chiyani Yesu poonetsa matamando athu? Paulo akuti, **“Chifukwa chake ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu**

nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mu-kazindikire chimene chili chifuno cha Mulungu, chabwi-no, ndi chokondweretsa, ndi changwiro” (Aroma 12:1, 2). Tiyeni tipereke matupi athu kwa Yesu pokhala moyo okondweretsa lye. Tiyeni timupatse nzeru zathu, kuganizira za dzina lake, mau ake ndi ntchito zake, m’malo moganizira zinthu zapadziko lapansi.

Ndizachidziwikire kuti ena akhoza kuona ngati kuti potumikira Mulungu mukutaya moyo wanu ndi mphatso (matalente) zomwe muli nazo. Kodi si Yudasi uja adaganiza kuti mphotho ya Maria inali yongotaya ndalamu? Koma Yudasi ali kuti le-ro? “**Amayesa wolungama wodala pomkumbukira; koma dzina la oipa lidzavunda**” (Miyambo 10:7). “**Wolungama adzakumbukika ku nthawi yosatha**” (Masalimo 112:6b).

Tikamaonetsa chikondi kwa abale a chikhristu ndiye kuti tikulemekeza Khristu yemwe amakhala mwa iwo. Kodi zomwe mumachitira makolo anu mwa Ambuye, ana anu, akazi kapena amuna anu ndi zomwe mukadamuchitira Yesu? Timalemekezanso Yesu pamene tikukonda adani athu, chifu-kwa amatiuza kuti tidzitero (Mateyu 5:44).

Khristu anatikonda kwambiri Kotero kuti anadziperekha yekha kwa ife. “**Choperekwa ndi nsembe kwa Mulungu, ikhale fungo ionunkhira bwino**” (Aefeso 5:2b). “**Potero mwa lye tipereke chiperekere nsembe yakuyamika Mulungu, ndiyo chipatso cha milomo yovomereza dzina lake**” (Ahebri 13:15).



Yohane 12:12-16

12M'mawa mwake khamu lalikulu la anthu amene adazza kuchikondwerero, pakumva kuti Yesu alinkudza ku

Yerusalemu, **13**anatenga makwata a kanjedza, natuluka kukakomana ndi Iye, nafuula, Hosana; wolemekezeka Iye wakudza m'dzina la Ambuye, ndiye mfumu ya Israele. **14**Koma Yesu, m'mene adapeza kabulu anakhala pamenepo; monga mulembedwa: **15**Usao-pe, mwana wamkazi wa Ziyoni; taona mfumu yako idza wokhala pa mwana wa bulu. **16**Izi sanazidziwa ophunzira ake poyamba; koma pamene Yesu analemekezedwa, pamenepo anakumbukira kuti izi zinalembedwa za Iye, ndi kuti adamchitira Iye izi.

Yesu adzabweranso monga mfumu yaulemerero

Mneneri wina mu Chipangano Chakale adati, “**Kondwera kwambiri, mwana wamkazi wa Ziyoni; fuula mwana wamkazi wa Yerusalem; taona, Mfumu yako ikudza kwa iwe; ndiye wolungama, ndi mwini chipulumutso; wofatsa ndi wokwera pa bulu, ndi mwana wamphongo wa bulu**” (Zekariya 9:9). Inde, kubwera kwa Yesu monga munthu, komanso ngati Mpulumutsi kunanenedwa kale lomwe momveka bwino ndi aneneri. Maulosi opitirira 300 anakwanirtsidwa kudzera m'moyo, imfa ndi kuukitsidwa

kwake kwa Yesu. Komabe maulosi oposera katatu kuchulukitsa ndi 300 aja *amayenera* kuti akwanirtsidwe pamene Yesu akubweranso ngati mfumu ya ulemerero pomwe akudzalamulira dziko lapansi (Chivumbulutso 20:4).

“Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mfuu, ndi mau a mngelo wamkulu, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Khristu adzayamba kuuka; pamene po ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse” (1 Atesalonika 4:16, 17).

“Vumbulutso la Ambuye Yesu wochokera Kumwamba pamodzi ndi angelo a mphamvu yake, m'lawi lamoto, ndi kubwezera chilango kwa iwo osamdziwa Mulungu, ndi iwo osamvera Uthenga Wabwino wa Ambuye wathu Yesu” (2 Atesalonika 1:7b, 8).

Kodi mwakonzekera kubwera kwake?

Mulungu amasunga malonjezano ake nthawi zonse. Iye akuchedwa kubwera ndi cholinga chakuti anthu ambiri apulumutsidwe. Iye **“wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa”** (2 Petro 3:9b). Komatu lye akubweranso posachedwa! Kodi mwakonzeka kukhala moyo wachiyero ndi kubweretsa ena kwa lye? **“Koma tsiku la Ambuye lidzadza ngati mbala; m'mene miyamba idzapita ndi chibumo chachikulu, ndi zam'mwamba zidzakananga nuka ndi kutentha kwakukulu, ndipo dziko ndi ntchito zili momwemo zidzatenthedwa. Popeza izi zonse zidzakananga nuka kotero, muyenera inu kukhala anthu otani nanga, m'mayendedwe opatulika ndi m'chipe-mbedzo”** (2 Petro 3:10, 11).



Yohane 12:24-26

24Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Ngati mbeu ya tirigu siigwa m'nthaka, nifa, ikhala pa yokha iyo; koma ngati ifa,

ibala chipatso chambiri. **25**Iye wokonda moyo wake adzau-taya; ndipo wodana ndi moyo wake m'dziko lino lapansi adzausungira kumoyo wosatha. **26**Ngati wina anditumikira Ine, anditsate; ndipo ku-mene kuli Ine, komwekonso kudzakhala mtumiki wanga. Ngati wina anditumikira Ine, Atate adzamchitira ulemu iyeyu.

Tanthauzo la kufa

Kufa kumabwera mphamvu ya chiukitso isanafike. Izi zinachitikanso ndi Khristu, kwa ife ifenso ndi chimodzimodzi. Mtumwi Paulo anationetsa tanthauzo la kufa kwa ife eni chifukwa cha Khristu. **“Komatu zonse zimene zinandipindulira, zomwezo ndinaziyesa chitayiko chifukwa cha Khristu. Kuti ndimzindikire lye, ndi mphamvu ya kuuka kwake”** (Afilipi 3:7, 10a).

Nthawi zambiri kumvera Khristu kumatanthauza kufa ku zilakolako zathu. Koma ife tikafa ku zimenezo, mphamvu ya Khristu mwa ife imayamba kugwira ntchito. Timaona umunhu wathu ukupachikidwa naye Khristu umunhu wathu wa-tsopano umakhala ndi moyo mwachikhulupiriro pamene ti-kuyenda mwa chikhulupiriro. **“Ndinapachikidwa ndi Khristu; koma ndili ndi moyo; wosatinso ine ai, koma Khristu ali ndi moyo mwa ine; koma moyo umene ndili nao tsopano m'thupi, ndili nao m'chikhulupiriro cha Mwana wa Mulungu, amene anandikonda, nadzipereka**

yekha chifukwa cha ine" (Agalatiya 2:20). "**Pakuti ngati mukhala ndi moyo monga mwa thupi, mudzafa; koma ngati ndi mzimu mufetsa zochita zake za thupi, mudzakhala ndi moyo**" (Aroma 8:13). Mulole Mzimu wa Mulungu ukutsogolereni pa zomwe ziyenera kufa mwa inu. Zizolowezi zoipa, kabenanso maganizo ena oipa. Pamene mwapanga *chisankho* chakuzyesera izi zakufa ndi kusachokamo mwa kumvera, mudzaona mphamvu ya Mulungu ikukutengerani ku moyo watsopano, kukupatsani mphamvu yokhala ndi zilakolako zatsopano, maganizo atsopano, ndikukupatsani moyo wa chigonjetso. "**Pakuti wakuchita mwa inu kufuna ndi kuchita komwe, chifukwa cha kukoma mtima kwake, ndiye Mulungu**" (Afilipi 2:13).

PHUNZIRO 21. YESU APHUNZITSA POPEREKA CHITSANZO NDI MALAMULO

Yohane 13:3-17, 34, 35

³Yesu, podziwa kuti Atate adampatsa Iye zonse m'manja mwake, ndi kuti anachokerwa kwa Mulungu, namuka kwa Mulungu, ⁴ananyamuka pamgonero, navula malaya ake; ndipo m'mene adatenga chopukutira, anadzimanga m'chuuno. ⁵Pomwepo anathira madzi m'nsambidwe, nayamba kusambitsa mapazi a ophunzira ake, ndi kuwapukuta ndi chopukutira, chime ne anadzimanga nacho.



⁶Anadza pomwepo kwa Simoni Petro. Iyeyu ananena ndi Iye, Ambuye, kodi Inu mudisambitsa ine mapazi?

⁷Yesu anayankha nati kwa iye, Chimene ndichita Ine su-chidziwa tsopano; koma udzadziwa m'tsogolo mwake. ⁸Petro ananena ndi Iye, Simudzasambitsa mapazi anga ku-nthawi yonse. Yesu anamanya-nkha iye, Ngati sindikusam-bitsa iwe ulibe cholandira pamodzi ndi Ine. ⁹Simoni Pe-tro ananena ndi Iye, Ambuye, si mapazi anga okha, koma-nso manja ndi mutu. ¹⁰Yesu ananena naye, Amene anatha kusamba alibe kusowa koma kusamba mapazi, koma ayera monse: ndipo inu ndinu oye-ra, koma si nonse ai. ¹¹Pakuti anadziwa amene adzampere-ka Iye; chifukwa cha ichi ana-ti, Simuli oyera nonse. ¹²Pa-menepo, atatha Iye kusambi-tsas mapazi ao, ndi kutenga malaya ake, anaseamanso, na-ti kwa iwo, Nanga chimene ndakuchitirani inu, muchizi-ndikira kodi? ¹³Inu mundi-

tcha Ine Mphunzitsi, ndi Ambuye: ndipo munena bwi-no; pakuti ndine amene. ¹⁴Chifukwa chake, ngati Ine Ambuye ndi Mphunzitsi, nda-sambitsa mapazi anu, inunso muyenera kusam-bitsana ma-pazi wina ndi mnzake. ¹⁵Pa-kuti ndakupatsani inu chi-tsanzo, kuti, monga Ine ndakuchitirani inu, inunso muchite. ¹⁶Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Kapolo sali wamkulu ndi mbuye wake; kapena mtumwi sali wamkulu ndi womtuma iye. ¹⁷Ngati mudziwa izi, odala inu ngati muzichita.

³⁴Ndikupatsani inu lamulo latsopano, kuti mukondane wina ndi mnzake; monga ndakonda inu, kuti inunso mukondane wina ndi mnzake. ³⁵Mwa ichi adzazindikira onse kuti muli ophunzira anga, ngati muli nacho chikondano wina ndi mnzake.

Zoti muchite

Kodi ndi zinthu ziti ziwiri zimene Yesu anaphunzitsa po-perekwa zitsanzo za Iye mwini?

1. Iye anati, "Ngati ine Ambuye ndi Mphunzitsi wanu _____ inunso muyenera" (vesi 14).
2. Iye ananenanso kuti, "Ndikukupatsani inu lamulo latsopano kuti _____ monga _____ kuti inunso mukondane wina ndi mnzake" (34).

Chinsinsi cha chisangalalo

Yesu anati tidzakhala moyo wachisangalalo ngati titatsatira chitsanzo chake ndi kutumikira ena. Koma ndiye chithunzi chabwino! Kumuona Mulengi akuwerama ndi kudzichepetsa kugwira ntchito ya kapolo natsuka fumbi la kumapazi a ophunizira ake! "**Mukhale nao mtima m'kati mwanu umene unalinso mwa Khristu Yesu, ameneyo, pokhala nao maonekedwe a Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofana ndi Mulungu, koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe a kapolo, nakhala m'mafanizidwe a anthu; ndipo popezedwa m'maonekedwe ngati munthu, anadzichepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda. Mwa ichinso Mulungu anamkwezetsa lye,...**" (Afilipi 2:5-9).

Tiyeni tilingalire njira zoti nkutumikira ena ndi kukumana ndi zosowa zao. Ngati titachita izi, tidzakhala okondwera. Kutumikira ndi kukonda ena kumaonetsa kuti ndifedi otsatira a Khristu chifukwa izi ndi zimene lye anachitira.

1. Yohane 14:1-3, 6

1Mtima wanu usavutike; mukhulupirira Mulungu, khulupirirani Inenso. **2**M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ngati sikudali kutero, ndikadakuzzani inu; pakuti ndipita kukonzerani inu malo. **3**Ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, mukakhale inunso. **6**Yesu ananena naye, Ine ndine njira, ndi choonadi, ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine.

2. Yohane 14:12

12Indetu, indetu, ndinena kwa inu, Wokhulupirira Ine, ntchito zimene ndichita Ine adzazichitanso iyeyu; ndipo adzachita zoposa izi; chifukwa ndipita Ine kwa Atate.

3. Yohane 14:13, 14

13Ndipo chimene chilicho-nse mukafunse m'dzina langa, ndidzachichita, kuti Atate



akalemekezedwe mwa Mwana. **14**Ngati mudzapempha kantu m'dzina langa, ndidzachita.

4. Yohane 14:15-17

15Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga. **16**Ndipo Ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe ina, kuti akhale ndi inu kunthawi yonse, **17**ndiye Mzimu wa choonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona Iye, kapena kumzindikira Iye. Inu mumzindikira Iye; chifukwa akhala ndi inu nadzakhala mwa inu.

²⁷Mtendere ndikusiyirani | inu monga dziko lapansi lipa-
inu, mtendere wanga ndiku- | tsa. Mtima wanu usavutike,
patsani; Ine sindikupatsani | kapena usachite mantha.

1. Yesu analonjeza **kukawakonzera malo** iwo akumutsatira (Yohane 14:1-3, 6).
2. Yesu analonjeza **mphamvu yopambana** chifukwa ankapita kwa atate. Mzimu wake wokhala mwa okhulupirira adzakhala ndi kuthekera kochita zinthu zopambana zomwe Yesu monga munthu m'modzi sadakachita pomwe anali padziko lapansi (Yohane 14:12).
3. Yesu analonjeza zokoma **zopambana zopezeka mu pemphero** kwa anthu ake (Yohane 14:13, 14).
4. Yesu analonjeza **kupezeka kopambana** ndi ophunzira aliyense. Pamene Mzimu Woyeranabwera, Yesu adzakhala *mwa ophunzira aliyense*, osati kungokhala *ndi* iwo chabe (Yohane 14:15-17).
5. Yesu analonjeza **mtendere wopambana** womwe dziko lidakaperekwa (Yohane 14:27). Sitiyenera kuchita mantha chifukwa “**lye wakukhala mwa inu aposa iye wakukhala m'dziko lapansi**” (1 Yohane 4:4b).

Zoti muchite

- A. Muwerengenso mavesiwa mosamalitsa, muwamve mauwo ngati kuti Yesu akuyankhula *ndi inu*. Mulembe pa pepala zonse zimene Yesu akunena kuti lye kapena Mzimu Woyeranadzakuchitirani *inuyo*.

B. Musankhe mavesi atatu omwe ali opambana kwa inu ochokera mu Yohane 14. Ndipo muwaloweze pamtima. Lembani mavesiwo m'munsimu:

PHUNZIRO 23. NKHANI YA MPESA



Yohane 15:1-11

1Ine ndine mpesa weniweni, ndipo Atate wanga ndiye wa-m'munda. **2**Nthambi iliyonse ya mwa Ine yosabala chipatso, aichotsa; ndi iliyonse yakuba-la chipatso, aisadza, kuti ika-bale chipatso chochuluka. **3**Mwakhala okonzeka tsopano inu chifukwa cha mau amene

ndalankhula ndi inu. **4**Khalani mwa Ine, ndi Ine mwa inu. Monga nthambi siingathe kubala chipatso pa yokha, ngati siikhala mwampesa; motere mulibe inunso ngati si-mukhala mwa Ine. **5**Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zake: wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala chipatso chambiri; pakuti kopanda Ine si-mungathe kuchita kanthu. **6**Ngati wina sakhala mwa Ine, watayika kunja monga nthambi, nafota; ndipo azi-sonkhanitsa nazitaya kumoto, nazitenthala. **7**Ngati mukhala mwa Ine, ndi mau anga akha-la mwa inu, pemphani chili-chonse chimene muchifuna ndipo chidzachitika kwa inu. **8**Mwa ichi alemekezedwa

Atate wanga, kuti mubale chipatso chambiri; ndipo mudzakhala ophunzira anga. ⁹Monga momwe Atate wandumkonda Ine, Inenso ndakonda inu; khalani m'chikondi changa. ¹⁰Ngati musunga malamulo anga mudzakhala

m'chikondi changa; monga Iye ndasunga malamulo a Atate wanga, ndipo ndikhala m'chikondi chake. ¹¹Izi ndalankhula ndi inu, kuti chimwemwe changa chikhale mwa inu, ndi kuti chi-mwemwe chanu chidzale.

Kukhala mwa Khristu

Tikalndira chikhululukiro ndi kusambitsidwa ndiponso moyo watsopano kuchokera kwa Yesu kupylera mu kumukhulupirira, tiyenera *kupitiira* kukhala mumzimu m'moyo wathu wonse wa chikhristu. Tisamafanizire ndi komwe tingakhale chifukwa cha mphamvu ndi nzeru zathu. Paulo anati, “**Kodi muli opusa otere? Popeza mudayamba ndi Mzimu, kodi tsopano mutsiriza ndi thupi?**” (Agalatiya 3:3).

Nthawi zina Yesu amatilanga ndi cholinga “chotitengulira.” Izi zikutanthauza kuti nthawi zina timadutsa mu nyengo zovuta kapenanso kuyesedwa kumene. Koma cholinga chake ndi chotipanga ife *kukhala obala zipatso*. “**Chilango chilichonse, pakuchitika, sichimveka chokondwetsa, komatu chowawa; koma chitatha, chipereka chipatso cha mtendere, kwa iwo ozoloweretsedwa nacho, ndicho cha chilungamo**” (Ahebri 12:11).

Chipatso cha Mzimu ndi chiyani?

Paulo akutiua kuti “**Koma chipatso cha Mzimu ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiro, chifatso, chile-tso**” (Agalatiya 5:22, 23a). Pamene mukupempha Yesu kuti akutsukeni, komanso ngati tsiku ndi tsiku mukupempha kuti Mzimu wake ukudzazeni, moyo wanu udzayamba kubereka zipatso zabwino komanso zochuluka kwambiri. Zina mwa zipatso za chiyero ndi mtima woyamika ndi kuyimba nyimbo, mtima womvera, kubweretsa ena kwa Yesu, kupereka chuma chathu ku ntchito ya Mulungu, kusataya nthawi, kuyankhula mau a Mulungu molimba mtima, ndiponso kuona mapemphero athu akuyankhidwa.

Chenjezo loopsa

Ngati sitili mwa Khristu, Yesu akutichenjeza kuti tidzataidwa kunja ngati nthambi yodulidwa, youma ndi kuponyedwa ku moto. Ndi okhawo obala zipatso chifukwa chokhala mwa Khristu omwe ali ophunzira ake (mavesi 6 ndi 8). Mtumwi Yuda akutikumbutsa kuti, “**Ambuye, atapulumutsa mtundu wa anthu ndi kuwatulutsa m'dziko la Ejipito, anaononganso iwo osakhulupirira**” (Yuda 5b).

Ngakhale kuti sitingathe kubala zipatso tokha, ndi kwa-bwino kuona mau a Mulungu, monga momwe timadziyan'ang'anira pa kalilole kuti “**Dziyeseni nokha, ngati muli m'chikhulupiro, dzitsimikizeni nokha...kuti Yesu Khristu ali mwa inu?**” (2 Akorinto 13:5a).

Ngati mau a Yesu ali mwa ife, ndikumvera zomwe akutiua, tidzakhala mu chikondi chake. (Yohane 15:10) Ngati titdziwa kuti Mzimu Woyera uli mwa ife, ndikumvera zomwe akutiua, sitiyenera kuchita mantha chifukwa Mzimu Woyera ndi chitsimikizo komanso chizindikiro chakuti ndife ake. Kumbukirani kuti chikondi ndicho yesero lopambana. **“Mulungu ndiye chikondi, ndipo iye amene akhala m’chikondi akhala mwa Mulungu, ndipo Mulungu akhala mwa iye”** (1 Yohane 4:16b). Mulungu amakukondani koposadi! Mukhale mu chikondi chimenecho.

PHUNZIRO 24. KUSANKHIDWA KUKHALA ABWENZI

Yohane 15:12-17

¹²Lamulo langa ndi ili, kuti mukondane wina ndi mnzake, monga ndakonda inu. ¹³Palibe munthu ali nacho chikondi choposa ichi, chakuti munthu ataya moyo wake chifukwa cha abwenzi ake. ¹⁴Muli abwenzi anga inu, ngati muzichita zimene ndikulamulani inu. ¹⁵Sinditchanso inu akapolo; chifukwa kapolo sadziwa chimene mbuye wake achita; koma ndatcha inu abwenzi;

chifukwa zimene ndazi-mva kwa Atate wanga ndakudziwitsani. ¹⁶Inu simuna-ndisankha Ine, koma Ine ndinakusankhani inu, ndipo ndinakuikani, kuti mukamuke inu ndi kubala chipatso, ndi kuti chipatso chanu chikhale; kuti chimene chilichonse mu-kapempha Atate m’dzina langa akakupatseni inu. ¹⁷Zinthu izi ndilamula inu, kuti mukondane wina ndi mnzake.

PHUNZIRO 25. YESU ATIPHUNZITSA KUYEMBEKEZA MAZUNZO

Yohane 15:18-25

¹⁸Ngati dziko lapansi lida inu, mudziwa kuti lidada Ine lisanayambe kuda inu. ¹⁹Mukadakhala a dziko lapansi, dziko lapansi likadakonda zake za lokha; koma popeza simuli a dziko lapansi, koma Ine ndinakusankhani inu mwa dziko lapansi, chifukwa cha ichi likudani inu. ²⁰Kumbukirani mau amene Ine ndinanena kwa inu, Kapolo sali wamkulu ndi mbuye wake. Ngati anandilondalonda Ine, adzakulondalondani inunso; ngati anasunga mau anga, adzasunga anunso. ²¹Koma izi

zonse adzakuchitirani chifukwa cha dzina langa, chifukwa sadziwa wondituma Ine. ²²Sindikadadza ndi kulanxhula nao sakadakhala nalo tchimo; koma tsopano alibe chowiringula pa machimo ao. ²³Iye wondida Ine, adanso Atate wanga. ²⁴Sindikadachit a mwa iwo ntchito zosachita wina, sakadakhala nalo tchimo; koma tsopano anaona, nada Ine ndi Atate wanganso. ²⁵Koma chitero, kuti mau olembedwa m'chilamulo chao akwaniridwe, kuti, Anandida Ine kopanda chifukwa.

Yohane 16:1-3, 33

¹Izi ndalankhula ndi inu kuti mungakhumudwitsidwe. ²Adzakutulutsani m'masunganoge, koma ikudza nthawi imene yense wakupha inu adzayesa kuti atumikira Muluungu. ³Ndipo izi adzachita, chifukwa sanadziwa Atate,

kapena Ine. ³³Zinthu izi ndalankhula ndi inu, kuti mwa Ine mukakhale nao mtendere. M'dziko lapansi mudzakhala nacho chivuto, koma limbikani mtima; ndalingonjetsa dziko lapansi Ine.

Zoti muchite

1. Dziko limadana ndi anthu otsatira Yesu chifukwa sali a
(15:19).
2. Yesu anati, "lye wondida Ine, adanso _____
wanga" (15:23).
3. Ngakhale kuti Yesu anagwira ntchito zopambana
m'mene anali padziko lapansi, dziko lapansi lopanda chi-
khulupiliro lili ndi _____ komanso
Yesu ndi Atate omwe (15:24).
4. Dziko limadana naye Yesu popanda _____ (15:25).
5. Nthawi ikubwera imene iwo _____
Akhristu adzaganiza kutiaku _____ (16:2).
6. Adzachita zinthu zoipa kwambiri chifukwa sana
Atate ndi Yesu (16:3).
7. Ngakhale tili nao mazunzo padziko lapansi, tikhoza
kukhala nacho chimwemwe, chifukwa Yesu _____
dziko lapansi (16:33).

PHUNZIRO 26. YESU AMATIPEMPHERERA

Yohane 17:1-8, 15-26

**¹Zinthu izi analankhula Ye-
su; ndipo m'mene anakweza
maso ake Kumwamba, anati,
Atate, yafika nthawi; leme-
kezani Mwana wanu, kuti
Mwana wanu akulemekezeni
Inu; ²monga mwampatsa Iye
ulamuliro pa thupi lililonse,**

kuti onse amene mwampatsa
Iye, awapatse iwo moyo wosa-
tha. ³Koma moyo wosatha ndi
uwu, kuti akadziwe Inu Mu-
lungu woona yekha, ndi Yesu
Khristu amene munamtuma.
⁴Ine ndalemekesa Inu pa
dziko lapansi, m'mene ndina-
tsiriza ntchito imene muna-

ndipatsa ndichite. ⁵Ndipo tso-pano, Atate Inu, lemekezani Ine ndi Inu nokha ndi ule-merero umene ndinali nao ndi Inu lisanakhale dziko lapansi. ⁶Ndalionetsera dzina lanu kwa anthu amene mwandipatsa Ine m'dziko lapansi; anali anu, ndipo mwandipatsa Ine iwo; ndipo adasunga mau anu. ⁷Azindikira tsopano kuti zinthu zilizonse zimene mwandipatsa Ine zichokera kwa Inu; ⁸chifukwa mau amene munandipatsa Ine ndinapatsa iwo; ndipo analandira, nazi-ndikira koona kuti ndinatulu-ka kwa Inu, ndipo anakhu-lupirira kuti Inu munandituma Ine. ¹⁵Sindipempha kuti muwachotse iwo m'dziko lapansi, koma kuti muwasunge iwo kuletsa woipayo. ¹⁶Siali a dziko lapansi monga Ine si-ndili wa dziko lapansi. ¹⁷Patulani iwo m'choonadi; mau anu ndi choonadi. ¹⁸Monga momwe munandituma Ine kudziko lapansi, Inenso ndi-natuma iwo kudziko lapansi. ¹⁹Ndipo chifukwa cha iwo Ine ndidzipatula ndekha kuti iwo-nso akhale opatulidwa m'cho-



onadi. ²⁰Koma sindipempherra iwo okha, komanso iwo akukhulupirira Ine chifukwa cha mau ao; ²¹kuti onse aka-khale amodzi, monga Inu Ata-te mwa Ine, ndi Ine mwa Inu, kuti iwonso akakhale mwa Ife: kuti dziko lapansi lika-khulupirire kuti Inu munandituma Ine. ²²Ndipo uleme-rero umene mwandipatsa Ine ndapatsa iwo; kuti akhale amodzi, monga Ife tili mmodzi; ²³Ine mwa iwo, ndi Inu mwa Ine, kuti akhale angwiro mwa mmodzi; kuti dziko lapansi lizindikire kuti Inu munandituma Ine, nimunawa-konda iwo, monga momwe munakonda Ine. ²⁴Atate,

amene mwandipatsa Ine, ndifuna kuti, kumene ndili Ine, iwonso akhale pamodzi ndi Ine; kuti ayang'anire ulememero wanga, umene mwandipatsa Ine; pakuti munandikonda Ine lisanakhazikike dziko lapansi. ²⁵Atate wolumgama, dziko lapansi sili-

nadziwa Inu, koma Ine ndinadziwa Inu; ndipo iwo anazindikira kuti munandituma Ine; ²⁶ndipo ndinazindikiritsa iwo dzina lanu, ndipo ndidzalizindikiritsa; kuti chikondi chimene munandikonda nacho chikhale mwa iwo, ndi Ine mwa iwo.

Yesu amakupemphererani inu

Yesaya m'mneneri analosera za Mesiya kuti "**napembedzera olakwa**" (Yesaya 53:12b). Anafuna kupereka moyo wosatha kwa anthu ambiri (Yohane 17:2) omulandira lye.

Yesu anawapemphererano ophunzira ake. Apa nkuti atamuza kale Petro kuti, "**Simoni, Simoni, taona, Satana anafunsa akutengeni kuti akupeteni ngati tirigu; koma ndinakupempherera kuti chikhulupiriro chako chingazime**" (Luka 22:31, 32a). Panonso asanafe, Yesu anawapempherera ophunzira ake kuti atalikirane ndi Satana woipayo. Akupemphererano onse omwe adzakhulupirire Yesu ngakhale m'badwo wa mtsogolo chifukwa cha umboni omwe anauwona ophunzira ake. Ankapemphererano *inu!*

Amakupemphererani nthawi zonse! "**Kuchokera komweko akhoza kupulumutsa konsekone iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa lye, popeza ali nao moyo wake chikhaliire wa kuwapembedzera iwo**" (Ahebri 7:25). Koma ndiye tili ndi mpulumutsi wabwino! Omatipempherera kuti tikhale naye pamodzi mchikondi! Mapemphero ake ndi oyankhidwa m'moyo mwanu ndinso m'banja mwanu lero.

Pambuyo pake Yesu ankapemphera mu Getsemane ndipo anapempherera ophunzira ake. Kenaka anawafunsa nati, “**Nkutero kodi? Simukhoza kuchezera ndi Ine mphindi imodzi?**” (Mateyu 26:40b). Kodi nthawi zina mumakhala panokha nkumalingalira za Yesu tsiku ndi tsiku, kupempherera otayika? Ndi chinthu chamtengo wapatali kukumana *naye* maso ndi maso pa “mpando wachifumu” wa chisomo tsiku ndi tsiku! “**Potero tilimbike mtima poyandikira mpando wachifumu wachisomo, kuti tilandire chifundo ndi kupeza chisomo cha kutithandiza nthawi yakusowa**” (Ahebri 4:16).

PHUNZIRO 27. YESU ANALI NDI MPHAMVU PA MOYO NDI IMFA YAKE

Yohane 10:17, 18

17Chifukwa cha ichi Atate andikonda Ine, chifukwa nditaya Ine moyo wanga, kuti ndikautengenso. **18**Palibe wi na andichotsera uwu, koma ndiutaya Ine ndekha. Ndili nayo mphamvu yakuutaya, ndi mphamvu ndili nayo yakuutenganso; lamulo ili ndinalandira kwa Atate wanga.

Yohane 19:4-11

4Ndipo Pilato anatulukanso kunja, nanena nao, Taonani, ndidza *naye* kwa inu kunja



kuti mudziwe kuti sindipeza mwa Iye chifukwa chilichonse. **5**Pamenepo Yesu anatuluka kunja, atavala korona waminga, ndi malaya achi-bakuwa. Ndipo ananena nao,

Taonani munthuyu! ⁶Ndipo pamene ansembe aakulu ndi anyamata anamuona Iye, ana-fuula nanena, Mpachikeni, mpachikeni. Pilato ananenana nao, Mtengeni Iye inu nimumpachike; pakuti ine sindipeza chifukwa mwa Iye. ⁷Ayuda anamyankha iye, Tili nacho chilamulo ife, ndipo monga mwa chilamulocho ayenera kufa, chifukwa anadziyesera Mwana wa Mulungu. ⁸Ndipo pamene Pilato anamva mau awa, anaopa koposa. ⁹Ndipo analowanso ku

Pretorio, nanena kwa Yesu, Muchoka kuti? Koma Yesu sanamyankha kanthu. ¹⁰Chifukwa chake Pilato ananena kwa Iye, Simulankhula ndi ine kodi? Simudziwa kodi kuti ulamuliro ndili nao wakukumasulani, ndipo ndili nao ulamuliro wakukupachikani? ¹¹Yesu anamyankha iye, Simukadakhala nao ulamuliro uliwonse pa Ine, ngati sukadapatsidwa kwa inu kuchokera Kumwamba; chifukwa cha ichi iye wondipereka Ine kwa inu ali nalo tchimo loposa.

Kodi Yesu adakafa?

Poganzira kuti Yesu analidi Mwana wa Mulungu, kodi kuanalidi kotheka kuti anthu nkumupha? Panalibe munthu amene anali ndi mphamvu yomuposa. Iye adakatha kusankha kufa kapena kukhala ndi moyo.

Yesu anamuua Pilato kuti, “...Ufumu wanga suli wa dziko lino lapansi; ufumu wanga ukadakhala wa dziko lino lapansi, anyamata anga akadalimbika nkhondo, kuti ndisaperekedwe kwa Ayuda... (Yohane 18:36). Yesu analola kuti agwidwe ndi Ayuda. Atagwidwa anati, “Kapena uganiza kuti sindingathe kupemphera Atate wanga, ndipo Iye adzanditumizira tsopano lino mabungwe a angelo oposa khumi ndi awiri? Koma pakutero male-

mbo adzakwaniridwa bwanji, pakuti kuyenera chomwecho?" (Mateyu 26:53, 54). Angelo omwe anatumikira Yesu pamene ankapemphera m'munda wa Getsemane adakatha kuwaononga asilikali omwe adamugwira iye. Koma Yesu anadziwa cholinga cha Mulungu chomwe chinaululika m'malemba.

Yesu mwini anati, "**Kuyenera kuti Mwana wa Munthu amve zowawa zambiri, ndi kukanidwa ndi akulu, ndi ansembe aakulu, ndi alembi, ndi kuphedwa, ndi kuuka tsiku lachitatu**" (Luka 9:22). Mwaonatu, Yesu anafa chifukwa chinali chikonzero *cha Mulungu* choikika dziko lisanalengedwe (Chivumbulutso 13:8).

Chinali chikonzero cha Mulungu kuti Yesu akagonjetse imfa! "**Popeza tsono ana ndiwo a mwazi ndi nyama, lyenso momwemo adalawa nao makhalidwe omwewo kuti mwa imfa akamuononge iye amene anali nayo mphamvu ya imfa, ndiye mdierekezi; nakamasule iwo onse amene, chifukwa cha kuopa imfa, m'moyo wao wonse adamangidwa ukapolo**" (Ahebri 2:14, 15). Kodi mumaopa kufa? Yesu anafa kuti akuwomboleni! Inde, Yesu anasankha kupereka moyo wake chifukwa cha inu!

PHUNZIRO 28. YESU ANAPACHIKIDWA NDI KUIKIDWA M'MANDA

Yohane 19:17, 18, 30-37

¹⁷Ndipo anasenza mtanda yekha, natuluka kunka kuma-

lo otchedwa Malo a Bade, amene atchedwa m'Chihebri, Gologota: ¹⁸kumene anampa-

chika Iye; ndipo pamodzi ndi Iye awiri ena, chakuno ndi chauko, koma Yesu pakati. ³⁰Pamene Yesu tsono adalandira vinyo wosasayo anati, Kwatha; ndipo anawerama mutu, napereka mzimu. ³¹Pomwepo Ayuda, popeza panali tsiku lokonzera, kuti mitembo ingatsale pamtanda tsiku la Sabata, pakuti tsiku lomwelola Sabata linali lalikulu, anapempha Pilato kuti miyendo yao ithyoledwe, ndipo acho-tsedwe. ³²Chifukwa chake anadza asilikali nathyola miyendo ya woyambayo, ndi ya winayo wopachikidwa pamodzi ndi Iye; ³³koma posika kwa Yesu, m'mene anamuona Iye, kuti wafa kale, sanathyola miyendo yake; ³⁴koma mmodzi wa asilikali anamgwaza ndi nthungo m'nthiti yake, ndipo panatuluka pomwepo mwazi ndi madzi. ³⁵Ndipo iye amene anaona, wachita umboni, ndi umboni wake uli woona; ndipo iyeyu adziwa kuti anena zoonia, kuti inunso mu-kakhulupirire. ³⁶Pakuti izi zi-



nachitika, kuti lembo likwani-ridwe, Fupa la Iye silidzathyo-ledwa. ³⁷Ndipo linenanso lembo lina, Adzayang'ana pa Iye amene anampyoza.

Yohane 19:40-42

⁴⁰Pamenepo anatenga mtembo wa Yesu, nauzenenga ndi nsalu zabafuta pamodzi ndi zonunkhira, monga mwa maididwe a maliro a Ayuda. ⁴¹Koma kunali munda kumalo kumene anapachikidwako, ndi m'mundamo munali manda atsopano m'mene sanaikidwamo munthu aliyense nthawi zonse. ⁴²Pomwepo ndipo anai-ka Yesu, chifukwa cha tsiku lokonzera la Ayuda, pakuti mandawo anali pafupi.

Imfa ya Khristu siinabwere mwangozi

Mfundu yofunika pofuna kulimvetsetsa Baibulo ndi kuzindikira kuti mau onse a m'Baibuloli amafotokoza za Khristu. “**Ndipo anayamba kwa Mose, ndi kwa aneneri onse nawatanthauzira iwo m'malembo onse zinthu za lye yekha**” (Luka 24:27). Yesu amadziwa “**kuti ziyenera kukwanitsidwa zonse zolembedwa za Ine m'chilamulo cha Mose, ndi aneneri, ndi Masalimo**” (Luka 24:44b). “**Ndipo anawatsegulira mitima yao, kuti adziwitse malembo; ndipo anati kwa iwo, Kotero kwalembedwa, kuti Khristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lachitatu; ndi kuti kulalikidwe m'dzina lake kulapa ndi kukhululukidwa kwa machimo kwa mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu**” (Luka 24:45-47).

Chikonzero cha Mulungu ndi chopambana! Ngati muli ndi Baibulo, muwerenge mau amene ali m'munsimu ndipo muone m'mene Mulungu analiuzira dziko lapansi za chikonzero chake mu Chipangano Chakale komanso m'mene lye anakwaniritsira mauwa kotheratu. (Awa ndi maulosi ochepa chabe mwa maulosi 300 omwe aneneri analosela za kubwera kwa Yesu koyamba).

Satanaanasunga mokakamiza chilengedwe cha Mulu-nku, koma Mulungu anali nacho chikonzero cha chiombolo ndipo chikonzerocho *chinapambana!* Aliyense amene aku-funa kuomboledwa akhoza kumasulidwa ku nsinga za Satana *tsopano* lino!

CHOLINGA CHA MULUNGU PA YESU	UNENERI	KUKWANIRTSIDWA
"Mbeu ya mkazi" yolonjezedwa	Genesis 3:15	Agalatiya 4:4
"Mbeu ya Abrahamu"	Genesis 22:18	Machitidwe A
yolonjezedwa		Atumwi 3:25
Kubadwa mu Betelehemu	Mika 5:2	Mateyu 2:1
Wobadwa mwa namwali	Yesaya 7:14	Mateyu 1:18
Utumiki mu Galileya	Yesaya 9:1, 2	Mateyu 4:12-16
Kudzakhala Mneneri	Deuteronomo 18:15	Yohane 6:14
Kudzakhala Wansembe	Masalimo 110:4	Ahebri 6:20
Kudzakhala Mfumu	Yesaya 9:7	Yohane 18:36, 37
Kukanidwa ndi Ayuda	Yesaya 53:3	Yohane 1:11; 5:43
Kulowa mu Yerusalemu	Zekariya 9:9	Yohane 12:13-15
mwaulemerero		
Kuperekedwa ndi bwenzi	Masalimo 41:9	Marko 14:10
Kugulitsidwa ndi ndalamza siliva 30	Zekariya 11:12	Mateyu 26:15
Mboni zonama zinamunenera zabodza	Masalimo 27:12	Mateyu 26:60, 61
Kukhala chete pozengedwa mlandu	Yesaya 53:7	Mateyu 26:62, 63
Anamenyedwa ndi kuthiridwa malovu	Yesaya 50:6	Marko 14:65
Anapachikidwa limodzi ndi ochimwa	Yesaya 53:12	Mateyu 27:38
Manja ndi miyendo zinabayidwa	Masalimo 22:16	Yohane 20:27
Ananyozedwa ndi kutundudzidwa	Masalimo 22:6-8	Mateyu 27:39, 40
Anapatsidwa vinyo wosasa kuti amwe	Masalimo 69:21	Yohane 19:29
Anapempherera adani ake	Yesaya 53:12	Luka 23:34
Anabayidwa m'nthiti	Zekariya 12:10	Yohane 19:34
Fupa lake silinathyoledwe	Masalimo 34:20	Yohane 19:33
Kuikidwa m'manda pamodzi ndi olemera	Yesaya 53:9	Mateyu 27:57-60
Kuukitsidwa kwake	Masalimo 16:10	Mateyu 28:9
Kukweranso kumwamba kwake	Masalimo 68:18	Luka 24:50, 51

(Mukafuna nkhani yonse yonena za imfa ya Yesu, muwerenge Mateyu 26, 27, Marko 14 ndi 15, Luka 22 ndi 23, Yohane 18 ndi 19 ndi Masalimo 22.)

PHUNZIRO 29. YESU AUKA KWA AKUFA

Yohane 20:1-9

1Koma tsiku loyamba la Sabata anadza Maria wa Magdalala mamawa, kusanayambe kucha, kumanda, napenya mwala wochotsedwa kumanda. **2**Pomwepo anathamanga nadza kwa Simoni Petro ndi kwa wophunzira wina amene Yesu anamkonda, nanena nao, Anachotsa Ambuye kumanda, ndipo sitidziwa kumene ana-muika Iye. **3**Anatuluka tsono Petro ndi wophunzira winayo, nalinkupita kumanda. **4**Koma anathamanga onse awiri pamodzi; ndipo wophunzira wi-nayo anathamanga naposa Petro, nayamba kufika kumanda; **5**ndipo m'mene anawera-ma chosuzumira anaona nsalu zabafuta zitakhala, komatu sanalowamo. **6**Pamenepo ana-dzanso Simoni Petro aliku-



mtsata iye, nalowa m'manda; ndipo anaona nsalu zabafuta zitakhala, **7**ndi mlezo, umene unali pamutu pake, wosakha-la pamodzi ndi nsalu zabafu-ta, koma wopindika padera pamalo pena. **8**Pamenepo tso-no analowanso wophunzira winayo, amene anayamba ku-fika kumanda, ndipo anaona, nakhulupirira. **9**Pakuti kufiki-ra pomwepo sanadziwa lembo lakuti ayenera Iye kuuka kwa akufa.

Chifukwa chiyani kuuka kwa Yesu kuli kopambana

Kale kale Yobu anafunsa kuti, “**Atafa munthu, adzakha-lanso ndi moyo kodí?**” (Yobu 14:14a). Yankho lake linali lakuti: “**Koma ndidziwa kuti Mombolo wanga ali ndi**

moyo, nadzauka potsiriza pafumbi. Ndipo khungu langa litaonongeka, pamenepo wopanda thupi langa, ndidza-penya Mulungu” (Yobu 19:25, 26). Inde chifukwa chakuti lye ndi wamoyo, ifenso tidzakhala ndi moyo (Yohane 14:19).

“Pakuti anapachikidwa m’ufooko, koma ali ndi moyo mu mphamvu ya Mulungu. Pakuti ifenso tili ofooka mwa lye, koma tidzakhala ndi moyo pamodzi ndi lye, mu mphamvu ya Mulungu, ya kwa inu” (2 Akorinto 13:4).

Uthenga wabwino wonse wofotokozedwa ndi Paulo mwachidule mu ma vesi awiri otero: **“Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, chimenenso ndinalandira, kuti Khristu anafera zoipa zathu, monga mwa malembo; ndi kuti anaikidwa; ndi kuti anaukitsidwa tsiku lachitatu, monga mwa malembo”** (1 Akorinto 15:3, 4). Popanda kuuka kwa Yesu kwa akufa, tidakasowa uthenga woti nkulalikira ndipo tikanakhala opanda chiyembekezo. Tidakakhalabe m’machimo athu ndipo tikadafa. Koma tiyamike Mulungu chifukwa Yesu *ndi* wamoyo ndipo akhoza kukhalanso mwa *inu*. **“Koma ngati Mzimu wa lye amene adaukitsa Yesu kwa akufa akhalabe mwa inu, lye amene adaukitsa Khristu Yesu kwa akufa adzapatsanso moyo matupi anu akufa, mwa Mzimu wake wakukhala mwa inu”** (Aroma 8:11).

Tsopano tiyenera kukhala ndi moyo chifukwa cha lye

“Pakuti chikondi cha Khristu chitikakamiza; popeza taweruza chotero, kuti mmodzi adafera onse, chifukwa chake onse adafa; ndipo adafera onse kuti iwo akukhala ndi moyo asakhalenso ndi moyo kwa iwo okha, koma mwa lye amene adawafera iwo, nauka” (2 Akorinto 5:14, 15). Pamene tinali akufa m’machimo athu, Khristu anatifera

ife; tsopano tili ndi moyo chifukwa cha Mulungu. Mwa Iye ndife olengedwa mwa tsopano. Tisakhale ndi moyo mwa-tsopano mwa ife tokha koma mwa Mulungu. Inu siinunso a inu nokha. **“Pakuti munagulidwa ndi mtengo wake wapatali; chifukwa chake lemekezani Mulungu m’thupi lanu”** (1 Akorinto 6:20).

PHUNZIRO 30. YESU AONEKERA KWA MARIA

Yohane 20:11-17

11Koma Maria analikuima kumanda kunja, alikulira. Ndipo m'mene alikulira ana-werama chisuzumirire kumanda; **12**ndipo anaona angelo awiri atavala zoyer, aliku-khala mmodzi kumutu, ndi wina kumiyendo, kumene mtembo wa Yesu udagona. **13**Ndipo iwowa ananena kwa iye, Mkazi, uliranji? Ananena nao, Chifukwa anachotsa Ambuye wanga, ndipo sindi-dziwa kumene anamuika Iye. **14**M'mene adanena izi, ana-cheuka m'mbuyo, naona Yesu ali chilili, ndipo sanadziwa kuti ndiye Yesu. **15**Yesu ananena naye, Mkazi, uliranji? Ufuna yani? Iyeyu poyesa kuti ndiye wakumunda, ananena ndi Iye, Mbuye ngati mwa-

mnyamula Iye, ndiuzeni ku-mene mwamuika Iye, ndipo ndidzamchotsa. **16**Yesu anane-na naye, Maria. Iyeyu m'mene anacheuka, ananena ndi Iye m'Chihebri, Raboni; chimene chinenedwa, Mphunzitsi. **17**Yesu ananena naye, Usandikhudze, pakuti sinditha kukwera kwa Atate; koma pita kwa abale anga, ukati kwa iwo, Ndikwera kunka kwa Atate wanga, ndi Mulungu wanu.



Ulemu umene Yesu amapereka kwa amai

Panthawi yovuta kwambiri komanso nthawi ya chisangalalo chopambana, Yesu anaonetsa ulemu waukulu kwa amai. Pa nthawi yowawitsa ya kupachikidwa kwake, Yesu analankhula mokoma mtima kwa mai ake nawapereka mu chisamaliro cha m'modzi mwa ophunzira ake okondedwa, Yohane (Yohane 19:26, 27). Atagonjetsa kupyolera mukuka kwa akufa, anasankha *kuyamba* kuonekera kwa amai, Maria wina!

Amai okhulupirira Mulungu omwe, amakhulupirira Mulungu nakhala ndi mzimu wachifatso ndi "**wapatali pamaso pa Mulungu**" (1 Petro 3:4b.) Mulungu atalenga munthu mchifanizo chake, anawalenga iwo mwamuna *ndi* mkazi opanda choipa chilichonse kuti akaonetsera chikhaldwe chake (Genesis 1:27). Mu zauzimu, Mulungu sasankha kuchitira amuna zomwe sangachitire amai. "**Mwa izi adatipatsa malonjezano a mtengo wake ndi akulu ndithu; kuti mwa izi mukakhale oyanjana nao umulungu wake**" (2 Petro 1:4a). "**Muno mulibe mwamuna ndi mkazi; pakuti muli nonse mmodzi mwa Khristu Yesu**" (Agalatiya 3:28b). Mulungu amalemekeza amai kwambiri koteru kuti analamulira amuna kuti adzikonda akazi ao monga Mulungu anakondera mpingo, anapereka moyo wake chifukwa cha mpingowo (Aefeso 5:25). "**Koteronso amuna azikonda akazi ao a iwo okha monga ngati matupi a iwo okha. Wokonda mkazi wa iye yekha, adzikonda yekha**" (Aefeso 5:28). Mulungu amakonda kuti padzikhala umodzi pakati pa mwamuna ndi mkazi wake. Amadana ndi kulekana pa ukwati. "**Pakuti ndidana nako kuleka kumene, ati Yehova**

Mulungu wa Israele” (Malaki 2:16a). “Kwaniritsani chimwemwe changa, kuti mukalingalire mtima zomwezo, akukhala nacho chikondi chomwe, a moyo umodzi, olinalira mtima umodzi; musachite kanthu monga mwa chotetana, kapena monga mwa ulemerero wopanda pake, komatu ndi kudzichepetsa mtima, yense ayese anzake omposa iye mwini” (Afilipi 2:2, 3).

PHUNZIRO 31. YESU AONEKERA KWA OPHUNZIRA AKE

Yohane 20:19-22

19Pamenepo, pokhala madzulo, tsiku lomwelo, loyamba la Sabata, makomo ali chitsekere, kumene anakhala ophunzira, chifukwa cha kuopa Ayuda, Yesu anadza naimirira pakati pao, nanena nao, Mtendere ukhale ndi inu.

20Ndipo pamene adanena ichi, anaonetsa iwo manja ake ndi nthiti zake. Pamenepo ophunzira anakondwera pakuona Ambuye. **21**Chifukwa chake Yesu anatinso kwa iwo, Mtendere ukhale ndi inu; monga Atate wandituma



Ine, Inenso ndituma inu.

22Ndipo pamene anati ichi anawapumira, nanena nao, Landirani Mzimu Woyeria.

Zoti muchite

M'malo mosalembedwamo mulembe mau omwe Yesu analankhula.

1. " _____ ukhale ndi inu" (vesi 19).
2. "Monga Atate andituma ine, inenso _____" (21).
3. " _____ Mzimu Woyerā" (22).

PHUNZIRO 32. OPHUNZIRO OKAYIKA AKHULUPIRIRA



Yohane 20:24-29

24Koma Tomasi, mmodzi wa khumi ndi awiriwo, wotchedwa Didimo, sanakhala nao pamodzi, pamene Yesu anadza. **25**Chifukwa chake ophunzira ena ananena naye, Tamuona Ambuye. Koma iye anati kwa iwo, Ndikapanda kuona m'manja ake chizindikiro cha misomaliyo, ndi kui-ka chala changa m'chizindikiro cha misomaliyo, ndi kui-ka dzanja langa kunthiti

yake; sindidzakhulupirira. **26**Ndipo pakupita masiku asanu ndi atatu ophunzira ake analinso m'nyumbamo, ndi Tomasi pamodzi nao. Yesu anadza, makomo ali chitseke-re, naimirira pakati, nati, Mtendere ukhale ndi inu.

27Pomwepo ananena kwa Tomasi, Bwera nacho chala chako kuno, nuone manja anga, ndipo bwera nalo dzanja lako, nuliike kunthiti yanga, ndipo usakhale wosakhulupirira, koma wokhulupirira. **28**Tomasí anayankha nati kwa Iye, Ambuye wanga, ndi Mulungu wanga. **29**Yesu ananena kwa iye, Chifukwa wandiona Ine, wakhulupirira; odala iwo akukhulupirira, angakhale sanaona.

Dalitso lapadera

Yesu akunena kuti ngati mutakhulupirira mwa lye ngakhale musanamuone ndi maso anu mudzakhala ndi dalitso lapadera. Masiku ano timamudziwa Yesu. Timamudziwanso chifukwa cha mau ake omwe amalankhula nafe kudzera mu Baibulo.

Tsiku lina *tidzamuona*. “**Tidziwa kuti, pa kuoneka lye, tidzakhala ofanana ndi lye, Pakuti tidzamuona lye monga ali**” (1 Yohane 3:2b). “**Odala ali oyera mtima; chifukwa adzaona Mulungu**” (Mateyu 5:8). “**Taonani, adza ndi mitambo; ndipo diso lilitonse lidzampenya lye, iwonso amene anampyoza; ndipo mafuko onse a pa dziko adzamlira lye**” (Chivumbulutso 1:7a). Kodi mukadzakumana ndi Yesu, mudzakhala okondwera kapena achi-soni? Ngati Yesu ali Mbuye wanu ndi Mulungu wanu ngati momwe analili Tomasi, mudzakhala okondwera!

PHUNZIRO 33. YESU ALI MPHAMVU YA KUPEREKA

Yohane 21:2-6; 9-12; 15-17

²Anali pamodzi Simoni Petro, ndi Tomasi, wotchedwa Didimo, ndi Natanaele wa ku Kana wa ku Galileya, ndi ana a Zebedeo, ndi awiri ena a ophunzira ake. ³Simoni Petro ananena nao, Ndinka kuka-

sodza. Ananena naye, Ifenso tipita nawe. Anatuluka, nalo-wa m'ngalawa; ndipo m'usiku muja sanagwira kanthu. ⁴Koma pakuyamba kucha, Yesu anaimirira pambali pa nya-nja, komatu ophunzirawo nadziwa kuti ndiye Yesu.



⁵Yesu ananena nao, Ananu, muli nako kanthu kakudya kodi? Anamyankha Iye, Iai.

⁶Koma anati kwa iwo, Ponyani khoka kumbali ya dzanja lamanja ya ngalawa, ndipo mudzapeza. Pamene po anaponya, ndipo analibenso mphamvu yakulikoka chifukwa cha kuchuluka nsomba.

⁹Ndipo pamene anatulukira pamtunda, anapenya moto wamakala pomwepo, ndi kansomba kosanjikikako, ndi mkate. ¹⁰Yesu ananena nao, Tenganiko nsomba zimene mwazigwira tsopano. ¹¹Chifukwa chake Simoni Petro anakwera m'ngalawa nako kera khoka kumtunda lodzala ndi nsomba zazikulu, zana limodzi, ndi makumi asanu ndi zitatu; ndipo zingakhale

zinachuluka kotere, kokha sillinang'ambika. ¹²Yesu ananena nao, Idzani mufisule. Koma palibe mmodzi wa ophunzira anatha kumfunsa Iye, Ndinu yani? Podziwa kuti ndiye Ambuye.

¹⁵Ndipo pamene atafisula Yesu ananena kwa Simoni Petro, Simoni mwana wa Yona, kodi undikonda Ine koposa awa? Ananena ndi Iye, Inde, Ambuye; mudziwa kuti ndikukondani Inu. Ananena naye, Dyetsa anaankhosa anga. ¹⁶Ananena nayenso kachiwiri, Simoni mwana wa Yona, ukonda Ine kodi? Ananena ndi Iye, Inde, Ambuye; mudziwa kuti ndikukondani Inu. Ananena naye, Weta nkhosa zanga. ¹⁷Ananena naye kachitatu, Simoni mwana wa Yona, kodi undikonda Ine? Petro anamva chisoni kuti anati kwa iye kachitatu, Kodi undikonda Ine? Ndipo anati kwa iye, Ambuye, mudziwa Inu zonse; muzindikira kuti ndikukondani Inu. Yesu ananena naye, Dyetsa nkhosa zanga.

Bwerani mudzadye

Chithunzi chabwino pamene Yesu akutiitanira ku nkhoma-liro! Yesu anawatsogolera ophunzira ake ku malo komwe kunali *zabwino zochuluka*. Kodi ndinu a njala ndi ludzu la chilungamo? Yesu adati, “**Odala ali akumva njala ndi ludzu la chilungamo; chifukwa adzakhuta**” (Mateyu 5:6). Bwerani pamaso pake m’mawa uliwonse ku nkhomaliro ya uzimu, kudya mau ake, omwe amakhutitsa miyoyo yathu. Ambuye, Mulungu wanu amene wakutsogolerani kukutulu-tsani mu ukapolo akunena kuti, “**Yasamitsa pakamwa pako ndipo ndidzalidzaza**” (Masalimo 81:10b).

Ngati muli ake a Khristu, mukuitanidwano kuti “mubwere ndipo mudzadye.” Yesu asanabwerenso ku dziko lapansi monga MFUMU YA MAFUMU komanso MBUYE WA AMBUYE. Umodzi wake ndi okhulupirira womwe ndi wamuyaya udzakondwerera ndi phwando la ukwati limeneli.

Yohane akulemba kuti, “**Tikondwere, tisekerere, ndipo tipatse ulemerero kwa lye; pakuti wadza ukwati wa Mwanawankhosa; ndipo mkazi wake wadzikonzera. Ndipo anampatsa iye avale bafuta wonyezimira woti mbu; pakuti bafuta ndiye zolungama za oyera mtima** (Chivumbulutso 19:7, 8). Kodi ndinu okonzeka kubwera ku phwando limenelo? Kumbukirani kuti sitingavale chiyero chomwe chingatipangitse kukhala ovomerezeka ku phwando la ukwati limeneli. Pamaso pa Mulungu, “**Pakuti ife tonse takhala ngati wina amene ali wosakonzeka; ndi zolungama zathu zonse zili ngati chovala chodetsedwa**” (Yesaya 64:6). Yesu yekhayo ndiye chovala cha chiyero chomwe chingatiyenereze kubwera ku phwando limeneli.

“Ameneyo sanadziwa uchimo anamyesera uchimo m’malo mwathu; kuti ife tikhale chilungamo cha Mulungu mwa lye” (2 Akorinto 5:21). Uku ndiko kusinthana kopambana. Anachotsa machimo athu natipatsa chiyero chake m’malo mwake!

Dyetsani nkhosa zanga

Yesu atamaliza kukudyetsani, akufunanso inu mudyetse ena. Kodi inu mwadyetsedwa m’moyo mwanu pomwe mumaphunzira mau opezeka mu Baibulo la Yohane? Ndiye mugawane ndi ena zomwe Mulungu wakuphunzitsani. **“Wetani gulu la Mulungu lili mwa inu, ndi kuliyang'anira,...koma okhala zitsanzo za gululo”** (1 Petro 5:2, 3). Tikoza kudalitsanso ena pogawana ndi ena Mau a Mulungu komanso kukhala chitsanzo kwa iwo. **“Ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulani inu; ndipo onani, Ine ndili pamodzi ndi inu masiku onse”** (Mateyu 28:20).

POLEMBAPO

Mayankho a mafunso

Mayankho a mafunso a phunziro la Baibulo la Yohane ale-mbedwa m'munsimu kuti mudzitha kuonera mafunso olondora. Muonere pa tsamba lino *pokhapokha* mutamaliza kuyankha mafunso onse.

Tsamba 5, 6

1. Mulungu
2. ndiye Mulungu
3. moyo
4. mumdimba
5. Yohane
6. Ake a mwini yekha
7. ana a Mulungu
8. mwazi, thupi, munthu, Mulungu
9. thupi
10. pakati pa ife
11. kudzala, chisomo, chisomo
12. Mwana

Tsamba 11

1. mau, m'chipululu
2. Lungamitsani njira
3. patsogolo, pambuyo
4. Mwanawankhosa, Mulungu, tchimo, dziko
5. Israele
6. nkhunda, Mzimu Woyeria

Tsamba 18

1. Chimene chilichonse akanena kwa inu, chitani
2. ndendende

Tsamba 27, 28, 29

1. mkulu, usiku
2. mphunzitsi
3. sabadwa mwatsopano
4. madzi, Mzimu
5. thupi
6. mzimu
7. Mose, njoka
8. anakonda, asatayike, moyo
9. akaweruze, akapulumutse
10. saweruzidwa, sanakhulupirire
11. mdima, kuunika, zoipa, zingatsutsidwe
12. choonadi

Tsamba 36, 37, 38

1. Analema
2. Undipatse Ine ndimwe
3. Pakuti Ayuda sayenderana nao Asamariya
4. madzi amoyo
5. Yense wakumwako madzi awa adzamvanso ludzu.
Iye wakumwa madzi amene
Yesu adzampatse sadzamva
ludzu nthawi zonse.

6. Anakhala amuna asanu ndipo
amene anali kukhala sanalinso
mwamuna wake
7. kulambira
8. mumzimu ndi m'choonadi
9. anamuka kumudzi nakauza
anthu za Khristu
10. kuchita chifuniro cha lye
amene anamutuma ndi
kutsiriza ntchito yake
11. Mpulumutsi wa dziko lapansi

Tsamba 44

1. 38
2. kuchiritsidwa
3. tauka, nuyende
4. usachimwenso
5. (a) kuswa tsiku la Sabata
(b) kudziyesera wolingana
ndi Mulungu

Tsamba 55

1. mukhala, ophunzira
2. choonadi
3. kapolo
4. Mwana
5. mukadakonda
6. Mulungu
7. Chifuniro chake,
chipunzitsocho

Tsamba 58, 59

1. Yesu
2. anzake
3. Afarisi
4. Makolo ake
5. Wosaona uja
6. Yesu
7. Wosaona uja

Tsamba 82

1. ndasambitsa mapazi,
kusambitsana mapazi
2. ndakonda, mukondane

Tsamba 90

1. dziko lapansi
2. Atate
3. anaona, nada
4. chifukwa
5. wakupha, Mulungu
6. anadziwa
7. ndaligonjetsa

Tsamba 104

1. Mtendere
2. Ndituma inu
3. Landirani

Published in numerous languages by World Missionary Press, Inc., as God supplies funds in answer to prayer. **For questions or more information by country, visit: www.wmp-contacts.org**

Buku ili siloperekedwa kwa aliyense ayi. Ili ndilo buku lopatsidwa kwa okhawo amene ali ndi chidwi chophunzira MAU A MULUNGU pa iwo wokha kapena ngati gulu.

Laulere—Lisagulitsidwe

Unless otherwise stated all scripture text is taken from:

Buku Lopatulika ndilo Mau a Mulungu

Copyright © 2015 by the Bible Society of Malawi

Used by permission



World Missionary Press
PO Box 120
New Paris, IN 46553-0120 USA
www.wmpress.org

1-25

Read booklets online or by App
www.wmp-readonline.org

1321/2 Chichewa BSJ